


AHEBRI, MUTU WOYAMBA

 Ndipo kuti ndipereke—pang’ono... Ine ndikuganiza kuti palibe china chabwinoko, kwa ine, kuposa Mawu okha. “Chikhulupiroro chimadza pakumva, ndi kumva Mawu a Mulungu.”

² Lachitatu, ndi mwinamwake Lamlungu, umodzi wa utumiki wa Lamlungu, powapatsa abusa kupuma kwapang’ono pokha, chomwe iwo ali oyeneredwa iko, ndipo ndimaganza kuti ife tingotenga Bukhu mu Baibulo. Ife tinkachita izo, ndipo nthawizina kukhala chaka pa izo.

³ Ine ndikukumbukira nthawi ina ife tinakhala chaka chathunthu pa Bukhu la Chivumbulutso. Koma, o, mai, zinthu zomwe ife tinaphunzira, ndi momwe izo zinaliri zodabwitsa! Ndiye ife tinabwerera mmbuyo ndipo tinatenga Bukhu la Daniele, kapena Bukhu la Genesis, kapena Eksodo, ndipo tinkangozitunga izo, mutu ndi mutu, ndipo izo zinkangolumikiza Baibulo lonseli palimodzi. O, ine ndimangozikonda izo!

⁴ Kenako mtsogolo pang’ono, ife tidzayenera kuti tidzatenge... Ngati Ambuye apitirira kutidalitsa ndipo ife nkumapitirira, ife tidzalowa mu zinthu zina zakuya kwenikweni mkati umu, zakuya kwenikweni. Ndipo ife tizingopita kuchokera pa malo kupita ku malo, kudutsa mu Malemba, ndi izo.

⁵ Ndipo ine ndimakonda kulipanga Lemba kufanana ndi Lemba. Ndi momwe izo ziyenera kuti zizikhalira. Ndi chithunzi chimodzi chokha chachikulu chokongola. Ndipo mu Bukhu ili lomwe ife tikuliphunzira, ife tilowa mu, o, chipulumutso, ndi machiritso Auzimu, ndi zozizwitsa, ndi zifundo. Ndipo, o, chirichonse chikubwera mkati umu.

⁶ Ndipo mwinamwake pamene ine nditi ndidzafike pa malo pomwe ine ndidzayenera kuti ndidzafike ku misonkhano... Ine sindiri kudziwa konse basi kuti ndi liti pomwe ine nditi ndidzakhale ndiri ku msonkhano, kuitanidwira ku msonkhano, chifukwa ine sindimakhala ndi chirichonse chokhazikitsidwa mpaka ine basi nditamverera kutsogozedwa kuti ndichite chinthu chinachake. Ndipo izo mwinamwake usanafike mmawa, ine ndikhoza kuwuluka kupita ku California, mpaka ku Maine kapena kwinakwake, basi kumene Iye angandiitanire ine. Ndi chifukwa chake ine sindimakonza, maulendo aakulu aatali, chifukwa ine sindingakhoze kuchita izo. Utumiki wanga sunapangidwe mwanjira imeneyo, ndipo iwo wangokhala wosiyana.

⁷ Ndipo tsopano ine ndimabwera kunyumba kuti ndidzangopuma pang’ono. Ine ndataya mapaundi twente, mu

msonkhano watha uwu. Ndipo M'bale Mercier ndi M'bale Goad anali uko, kanthawi kapitako, ndipo anati, "M'bale Branham, ine ndazindikira zomwe inu mumachita. Inu mumaika mtima wanu wonse mu izo."

⁸ Ine ndinati, "Ndi njira yokha yomwe iwe ungakhoze kuchitira mtundu wa ntchito yabwino kwa Ambuye, ndi kuika chirichonse chomwe uli nacho kutsogolo komwe kwa Khristu; mphamvu zako zonse, solo yako yonse, mtima wako wonse, malingaliro ako onse, chirichonse chomwe iwe uli nacho." Pamene iwe ukuchita chirichonse, uzichichita icho molondola kapena usati uchichite konse icho, mukuona, ingozisiya izo zokha. Inu mukati mukhale Mkristu, ikani chirichonse chomwe inu muli nacho kwa Khristu, ndicho, nthawi yanu, luntha lanu, chanu chirichonse.

⁹ Ine ndikungomuzindikira mnyamata uyu. Uyo ndi mkazi wanu, M'bale Burns, ndi chomwecho, yemwe akusewera ndi kumaimba apo, banja laling'ono ilo. N—ndipo iyo si piano, ngakhalenso si limba, koma ndi mtundu wina wa ching'wenyeng'wenye, iwo akumachikhwatcha icho ndi kumakodola icho, ndi kuchitira chinachake kwa Ambuye. Ngati inu mungakhoze kuchita izo, ndi kuimba, ndiko, kupindula miyoyo. Muzichita chinachake, ziribe kanthu. Ngati i—inu mungakhoze kuimba muluzu, chabwino, ziimbani muluzu. Muzichita chinachake basi. Kungochitira umboni kapena kuchitira chinachake kwa Ufumu wa Mulungu. Chirichonse chomwe inu muli nacho, zichiikani icho mochigwiritsira ntchito ya Mulungu.

¹⁰ Tsopano, ife sitikuyesa kuti tikhale motalika kwambiri, chifukwa ine ndikudziwa kuti inu mumagwira ntchito. Inu muyenera kuti muwuke molawirira. Ndipo ine ndikupita kukasaka agologolo mmawa uliwonse. Ine ndingokuuzani inu choonadi. Ndi chimene ine ndikuchita. Ndi chimene ine ndimabwerera kwathu, kuti ndidzapume pang'ono. Ndipo chotero ine ndikumadzuka, pafupi foro koloko, ndi kumapita ku thengo uko ndi, chabwino, kusaka pang'ono pokha ndi kupita kukagona. Ndipo ine ndikuonjezera kulemera kwina kunja mobwezera, kotero ine ndikhala nditapuma, pakapita kanthawi, ngati inu. . . Ambuye akalola. Ndipo chirichonse chiri bwino.

¹¹ Chabwino, tsopano, ife tikuti mutembenuze mu Mabaibulo anu. Ine ndikufuna kuti inu muzibweretsa Mabaibulo anu usiku uliwonse, kuti inu. . .momwe inu mungathere. Ngati winawake akufuna ochepa, kodi winawake angafune kuti azitsatira limodzi ndi kuwerenga uku, ife tiri nawo ena apa, ife tikanakhala ndi. . .ena a othandizira kuti awapereke iwo. Aliyense akufuna limodzi? Chabwino, ingokwezani dzanja lanu.

¹² Ndikudabwa ngati M'bale. . .Doc, bwera kuno ndi kudzatenga Mabaibulo awa. Iwe waima pafupi ndi apo, ndi

M'bale Burns. Ndi kulondola uko, Burns? Ine ndinamumva iye akuti... [M'bale akuti, "Conrad."—Mkonzi.] Chiani? ["Conrad."] Conrad. Ine ndinamutcha iye... Ine ndikukhala ngati wovutikira kumva, mwinamwake, M'bale Neville. Kodi ine ndinalipeza motani dzina loti Burns? Ine ndikuidziwa nkhope ya mwamunayu, ndipo ine basi sindingathe, sindimakhoza kulitchula dzina lake.

¹³ Ndipo inu mukudziwa, pamene iwe umayamba kukula pang'ono, ine ndapeza chinthu chimodzi, ndi kovuta kwa ine kuti ndiwerenge Baibulo ili. Ndipo ine ndikungodana nazo kuganiza za kumavala magalasi, kuti ndiziwerenga Baibulo.

¹⁴ Koma, kuno si kale litali, ine ndinkaganiza kuti ine ndinali kuchita khungu. Ndipo ine ndinapita uko kukamuwona Sam. Ndipo Sam anati, "Bill, ine sindikudziwa." Anati, "Ine ndingokukonzerani inu kuti mukakomane ndi katswiri wina."

¹⁵ Ine ndinapita ku Louisville. Icho chiyenera kuti chinali chifuniro cha Ambuye. Katswiri wina wotchuka; ine ndaiwala dzina lake tsopano. Koma iye anali atawerenga bukhu langa. Ndipo iye anati, "Ngati inu muti mudzabwerere konse ku Afrika, ine ndikufuna kuti ndidzapite nanu." Iye anati, "Ndipo ngati inu... Anthu aku Afrika awo amakukondani inu." Ndipo anati, "Iwo ndi azamatsenga kwambiri, makamaka ndi mpeni, ukati uzicheka. Chotero," anati, "Ine ndikufuna kuti ndikapereke miyezi sikisi ya moyo wanga, ku oparashoni ya ng'ala ndi zinthu, kwa... mu mishoni." Ndipo anati, "Ngati ife tingakhoze kupita limodzi, ndipo inu mukhoza kukonedwa nawo, monga choncho." Anati, "Ndiye ngati iwo atati ali ndi ng'ala ndi ntchito ya maso," anati, "ine ndingakonde kumakangopereka izo, mwaulere, miyezi sikisi ya izo." Ndipo ine ndaiwala kuti iwe umayenera kuti uyembekezere motalika bwanji kuti ukomane naye iye.

¹⁶ Ndipo ife tinali titakhala mu kachipinda kakang'ono ndipo iko kanali—kuwala kwakung'ono kofiira kunayaka, kumbuyo uko mu chipinda chamdima. Bwanji, ine ndimakhoza kuwerenga zilembo izo. Izo zimati twente-twente. Ine ndimakhoza kuziwerenga izo mbali iliyonse. Ndipo iye anaziyika izo pa fifitini-fifitini, ndipo ine ndimakhoza kuziwerenga izo. Ndipo anaziika izo pa teni-teni, ndipo ine ndimakhoza kuziwerenga izo. Iye anati, "Chabwino, palibe vuto lalikulu ndi maso anu."

¹⁷ Kotero iye anali ndi choyang'anira patali chaching'ono. Iye anaika kachinthu kakang'ono kumbuyo kwake, kachinthu kakang'ono, inu mukudziwa. Zoyang'anira patali zakale zija, ndi angati akuzikumbukira konse izo? Ife tinkakonda kuyang'ana kupyolera mu izo, poyang'ana pa zithunzi, chonga ngati icho. Ndipo iye anati, "Kodi inu mungakhoze kuziwerenga izo?"

Ine ndinati, "Inde, bwana."

Iye anati, "Ndiwerengereni ine izo."

18 Izo zinali, o, ndime yonse, pafupi monga *choncho*. Ine ndinayamba, ndinawerenga izo; iye anayamba kuzikokera izo mmwamba, monga *choncho*, ndinayamba kumachedwera chedwera. Iye anafika monga *chonchi*, ine ndinaima. Iye anati, “Ndikhoza kukuuzani inu chinthu chimodzi, inu mwadutsa pa forte.”

Ine ndinati, “Eya, uko nkulondola, ndinadutsa kale izo.”

19 Iye anati, “Inu mwachita chotani izo?” Iye anati, “Diso la umunthu, mwachibadwa, pamene iwe ufika usinkhu za zaka forte, monga tsitsi lako limayamba imvi, ndi zina zotero, mpira wa m’diso umayamba kuphwa.” Anati, “Tsopano, ngati iwe ukhala moyo utali wokwanira, awo adzabwereranso kachiwiri.” Iye anati, “Kupenya kwachiwiri uko, iwo amakutcha iko. Koma,” anati, “munthu wokhalapo, wa pafupi usinkhu wa zaka forte, iwo makamaka...” Anati, “Palibe chovuta chirichonse ndi maso awo.”

20 Ine ndikhoza—ine ndikhoza kuliwona tsitsi ilo ngati ilo likanakhala liri pansu, ilo litathothoka pa ine. Koma likafika pafupi ndi ine...Ndipo iye anati, “Tsopano, inu mukamawerenga Baibulo lanu,” anati, “Inu mumalikankhira ilo kutali ndi inu.” Anati, “Pakapita kanthawi, nkono wanu sudzakhala wotalika mokwanira, mpaka inu si—simudzakhoza kuufikitsa iwo patali mokwanira kuti muligwire ilo.”

21 Ndipo kotere iye anandipangira ine magalasi, ndipo gawo lammusi iwe ukhoza, ndi lowerengera. Iye anati, “Tsopano, mu guwa lanu...” Iye ankaganiza kuti ine ndinali wina wa azilaliki olemekeseka awa kuno, inu mukudziwa. Ndipo kotero ananena kuti...inu...Gawo lapamwambalo ndi magalasi wamba achizolowezi, magalasi wamba chabe. Ndipo gawo lammusilo liri ndi mtundu wina wa kaperedwe mmenemo, kuti ine ndizikhoza kumawerengera izo pafupi, inu mukudziwa, monga *choncho*. Kotero ine ndimangodana nawo kuwavala iwo; ine ndithudi.

22 Ndipo tsopano, mu kuphunzitsa kwa Baibulo, ndipo ine ndiri ndi Chipangano Chatsopano usikuuno. Kotero ndizo...Ine ndiri ndi Chipangano Chatsopano cha Collins. Ilo liri ndi zodindidwa za usinkhu wabwino. Koma tsopano, pamene ine ndibwerera kwa linalo, i—ine ndimayenera kuti ndipite kwa amzanga akale aja, n—ndi kumakhala ngati kuwerenga kupyolera mwa iwo. Koma chirichonse chomwe izo ziri, i—ndine wokondwa kuti ndiri nacho chinachake chomwe i—ine ndingakhoze kuchiwerenga. Ndipo—n—ndipo chirichonse chomwe ine ndiri nacho, ine ndizimupatsa aliyense chirichonse chomwe ine ndingathe, kwa ulemerero wa Mulungu, ndikuyembekeza kuti Iye achichotsapo chizindikiro cha usinkhu ichi. Ine sindingakhoze kumufunsa Iye kuti achotsepo usinkhu wangawu. I...Inu mukudziwa, icho ndi chinthu chimodzi chokha chomwe ife tonse tiyenera kuchichita.

Ife tiyenera kuti tidutse mu izo. Ndipo ine ndikudziwa kuti ine sindiri mnyamata wamng'ono monga ine ndinaliri, ndikuima pano pa nsanja. Ine ndiri wa usinkhu wa zaka forte-eyiti. Ndipo tangoganizani, zaka ziwiri zoonjezera, ndidzakhala usinkhu wa zaka fifite, M'bale Mike.

²³ Mai, sindingakhoze kukhulupirira nkomwe izo! Ine basi . . . Ine sindinkadziwa kuti ine ndinali nditadutsa makumi awiri mpaka pafupi zaka ziwiri zapitazo. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Ine basi . . . Ine sindikukhoza kukhulupirira izo. Ndipo komabe i—ine . . . Ndi kovuta kuti ine ndikhulupirire mpaka nditayang'ana pa kalilole, ndiyeno i—ine ndikudziwa kuti izo ziri, ndiye. K—koma kuti ndizingoyang'ana, ine ndikungomverera kuti izi ziri bwino basi monga ine ndinayamba ndamvererapo mu moyo wanga, ndipo ndine wothokoza pa izo, naponso. Matamando onse akhale kwa Mulungu.

²⁴ Tsopano, ife tikuphunzira Bukhu la Ahebri. Ilo lakhala . . . O, ilo ndi limodzi la Mabuku okuya, olemera kwambiri a Baibulo. Ine ndikukuuzani inu, ndi Bukhu lomwe liti kwenikweni lidza . . . Ngati Mulungu alola, ndipo ife tikangolowa mu izi, ine ndikukhulupirira ife tidzapezamo mibulu ya golide mpaka ife tizingomafuula matamando a Mulungu nthawi zonse. Ndipo tsopano ine . . .

²⁵ Bukhu la Ahebri, kwenikweni chomwe Ilo liri, Ilo liyenera kuti linalembedwa ndi Paulo Woyera, wofotokoza za Baibulo wamkulu, ine ndikulingalira, dziko linayamba lakhalapo naye, kunja kwa Ambuye wathu Yesu Khristu. Ndipo Paulo anali kulekanitsa . . . Tsopano, Paulo anali mphunzitsi weniweni wa Baibulo; ilo ndi, Chipangano Chakale. Ndilo Bukhu lokha lomwe linali litalembedwa apo, lotchedwa Baibulo. Ndipo iye anali kuyesera kuti asonyeze kwa Ahebri, kulekanitsa Chipangano Chakale ndi kusonyeza Chipangano Chakale pokhala mthunzi kapena choimira cha Chatsopano.

²⁶ Apo pomwe ife tikhiza kukhudza mzere wapachimake ndi kukhala miyezi itatu apo pomwe pa lingaliro limodzi ilo, apo pomwe. Kuti tipite mmbuyo momwe, ngati ife tingakhoze kutembenezira mu Mabaibulo athu tsopano, chifukwa ife tiri pa Ahebri, mutu wa 1. Koma ngati ife tingatembenezire ku Chivumbulutso, mutu wa 12, inu mungaziwone izo mwangwiro kachiwiri, momwe mithunzi. Ngati . . . inu omwe muli ndi mapensulo anu ndipo mukuti muzilemba Malemba. Mu Aheb- . . .

²⁷ Mu Chivumbulutso 11, ife tikupeza kuti Yohane, pa chisumbu cha Patmo, anawona mkazi ataima mu mlengalenga, ndipo iye anali ndi dzuwa pa mutu pake ndi mwezi pansu pa mapazi ake. Ndipo mkaziyo anali mu kumva kuwawa, ali ndi mwana woti abadwe. Iye anabala mwana wamwamuna. Chinjoka chofiira chinaima, kuti chimulikhwire mwanayo

mwamsanga pamene iye akanabadwa. Ndipo—mwanayo anatengedwera Kumwamba, ndipo mkaziyo anathawira ku chipululu kumene iye anakadyetsedwa kwa nthawi, nthawi, ndi theka la nthawi, kapena kugawaniza kwa nthawi.

²⁸ Tsopano, mkaziyo ankaimira mpingo, ndipo Mwana yemwe iye anamubala anali Khristu. Mwezi pansi pa mapazi ake linali lamulo, dzuwa pa mutu pake chinali chisomo. Nyenyezi khumi ndi ziwiri mu nduwira yake zinali atumwi khumi ndi awiri. Ndipo apo ndi pamene, pa chiani. . . . Atumwi khumi ndi awiri anali ulemerero kapena kuveka nduwira kwa Chipangano Chatsopano. Mukuona? “Pakuti palibe maziko ena angakhoze kuikidwa kuposa awo omwe anaikidwa kale.” Mukuona? Izo, Maziko, c—Chipangano Chatsopano, atumwi, Chiphunzitsa cha atumwi, ndi zina zotero, ndi nduwira ya maziko a Chipangano Chatsopano. Ndiyeno pa. . .

²⁹ Mwezi ndi mthunzi wa dzuwa. Dzuwa limangonyezimiritsa kuwala kwake pamene ilo liri kuseri kwa dziko lapansi. Ndipo mwezi umapereka kuwala kwake, kuti tiziyenda nako, usiku. Ndipo ndi chithunzi chokongola bwanji chomwe ife tiri nacho apa, chithunzi china chokongola: dzuwa limaimira Khristu; m—mwezi umaimira Mpingo. Izo zangokhala ngati mwamuna ndi mkazake. Ndipo mu kusakhalapo kwa Khristu, Mpingo umanyezimiritsa Kuwala kwakung’onoko, Uthenga. Ndipo iko—ndiko Kuwala koti tiziyendamo mpaka Mwana atulukire kachiwiri, ndiye Mpingo ndi Mwana, mwezi ndi dzuwa, zikulumikizana palimodzi. Mukuona? Mwezi ndi gawo la dzuwa, ndipo Mpingo ndi gawo la Khristu. Ndipo pamene Khristu palibe, Mpingo umanyezimiritsa Kuwala Kwake. Ndiyeno motsimikiza monga momwe ife tingakhoze kuwonera mwezi ukuwala, iwo umadziwa dzuwa likuwala kwinakwake. Ndipo utati wonse pamene Mpingo ukunyezimiritsa Kuwala kwa Khristu, Khristu ali moyo kwinakwake. Ameni. Taganizani za izo.

³⁰ Tsopano, lamulo linali choimira cha chisomo, koma lamulo linalibe mphamvu yopulumutsira mwa ilo. Lamulo linali kokha. . . . Lamulo linali mpolisi. Mpolisi anakuikani inu mu ndende, koma, inu mukuona, izo zinatengera chisomo kuti chikutulutseni inu mu ndende. Mukuona?

³¹ Kotero Magazi a Khristu, Uthenga, amatiwombola ife kwa tchimo. Lamulo limangotipanga ife kukhala ochimwa. Lamulo linangoti, “Iwe ndi wochimwa. Iwe usati uziba. Iwe usati uzichita chigololo. Iwe usati uzichitira umboni wabodza.” Mukuona? Ilo ndi munthu waupolisi yemwe amanena kuti ndiwe wolakwa ndipo iwe walakwitsa. Koma Uthenga ndi nkhani yabwino. Khristu anafa kuti atipulumutse ife kwa zolakwitsa zathu zonse, zolakwira kwa lamulo. Khristu anafa kuti atitulutse ife uko.

³² Tsopano, Paulo, mwamsanga pamene iye anatembenuzidwa, iye sanakafunsire konse kwa seminare iliyonse, ngakhalenso sanakafunsire kwa atumiki aliwonse. Koma kodi inu munazindikira? Iye anapita uko mu Arabia, ndipo anali uko zaka zitatu, mu Arabia. Tsopano, izi ziri, mwa kulingalira kwanga, kuti. . .

³³ Tsopano, ife tiyenera kuti tipeze maziko a izi, kotero ife tidziwe kufunikira kwake kwa izi. Ndipo phunziro loyambali, usikuuno, ife tikutenga maziko athu.

³⁴ Tsopano, Paulo anali mphunzitsi wotero wa Baibulo, chifukwa iye anaphunzitsidwa pansu pa Gamalielo wamkulu, wotchuka wa nthawizonse uja. Ndipo iye anali mmodzi mwa odziwika kwambiri a tsikulo, mphunzitsi wamkulu uja wa lamulo ndi aneneri. Kotero, Paulo anali wophunzitsidwa bwino mu zinthu zimenezo.

³⁵ Ndiyeno ine ndimamukonda iye mwanjira iyi, vumbulutso lalikulu ili, pokhala woonamtima mu mtima mwake, wokupha, anali atavomerezera kwa imfa ya Stefano ndipo anamuwona Stefano akufa pansu pa miyala ndi mabuluma ali kugendedwa mpaka imfa. Ine ndikuganiza kuti izo ziyenera kuti zinamukhudza Paulo pamene iye anamuwona Stefano akukwezera manja ake Mmwamba, nati, “Ine ndikuwona Kumwamba kutatseguka. Ine ndikumuwona Yesu ataima pa dzanja lamanja la Mulungu.” Ndipo iye anati, “Atate, musati muike chiweruzo cha tchimo ili mowatsutsa iwo.” Ndipo iye anagona tulo.

³⁶ Kodi inu mumazindikira izo? Iye sanafe konse. Iye anagona tulo. Monga ngati. . . Ine sindikukhulupirira kuti iye anamverera konse mwala wina. Monga ngati mwana pa chilolo cha mayi wake, amagonera tulo, Stefano anagona tulo mu mikono ya Mulungu.

³⁷ Apo pali chinachake, kwa Paulo, chimene chinamukhudza iye. Ndiye iye, munthu aliyense pansu pa kutsutsidwa, amayesera kuti amenyane nacho Icho, iye akugubuduzikira mpaka kwa wansembe wamkulu ndi kukatenga makalata ena. Anati, “Ine ndikawamanga anthu onse awo omwe akupanga phokoso lonse ilo, ndi otengeka awo;” omwe ankalingaliridwa, chomwe ife tingachitche lero, “wotentheka mopitiriza,” wina kapena chinachake chonga izo, opanga phokoso lochuluka ndi kuyambitsa chisokonezo. “Ife tingopita uko ndi kukazithetsa izo.”

³⁸ Ndipo ali paulendo wake akupita, waung’ono wakale. . . osati msewu wawukulu kwambiri monga ife timayendamo. Ndipo misewu iyo mu Palestina, basi tinjira tating’ono, monga tinjira ta ng’ombe kodutsa mmitengo kumene ng’ombe, ndi nkhusa, ndi akavalo, ndi abulu, ndi ngamila, zinkapitira mmapiri.

39 Ndipo Paulo, ali paulendo wake waku Damasiko, pafupi masana, tsiku lina, Kuwala kwakukulu kunawalira pansi ndipo kunamukanthira iye pansi. Palibe yemwe anakuwona Iko koma Paulo. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire izo. Ndipo apa pomwe, ichi si cha ine tsopano, koma basi kuti ife titsogolere ku maziko awa. Kutu inu mudziwe kuti Yesu yemwe uja. . .

40 Tsopano, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikubwereranso kwa Mulungu.”

41 Tsopano, pamene Iye ankawatsogolera ana a Israeli, Iye anali Lawi la Moto. Ndipo Iye anapangidwa kukhala thupi, ndiye Iye anabwereranso ku Lawi la Moto lomwe lija. Ndipo pamene Iye anakomana ndi Paulo paulendo waku Damasiko, Iye anali Lawi la Moto lija, Kuwala kuja, mwaona, Kuwala kwakukulu. Ndipo Paulo anati, “Kodi ndi ndani Uyo yemwe ine ndikumuzunza?”

42 Iye anati, “Ine ndine Yesu, yemwe iwe ukumuzunza,” Kuwala. O, kodi Iye Si wodabwitsa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

43 Ndipo apa Iye ali, usikuuno, pomwe pano ndi ife. Anajambulitsa chithunzi Chake apo pomwe, Chinthu chomwecho, onani, Lawi la Moto, Kuwala, chimodzimodzi basi monga Iye anali, “Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

44 Tsopano amuna omwe anali ndi iye sanakuwone Kuwala uko, koma Iko kunali apo chimodzimodzi basi. Zotsatira zimapereka zofanana.

45 Tsopano, kodi ndi zotheka k—kutu winawake akhoza kumuwona Khristu mu chipinda chino ndipo osakhalapo wina womuwona Iye? Zedi. Izo zinachitika apo.

46 Izo zinachitika naponso usiku wina pamene Petro anali mu ndende. Ndipo Kuwala uko kunadza nikulowa mu ndende, ndipo kunamukhudza Petro, ndipo anayenda pafupi pomwe ndi mlonda wamkati, mlonda wakunja, anayenda kudutsa pa chipata, chipata chachikulu, ndi chipata cha mzinda. Petro anati, “Ine ndiyenera kuti ndimalota.” Koma iye anayang’ana pozungulira, koma Kuwala kunali kutapita; Khristu, Wamuyaya uyo, Kuwala kwanthawizonse. Apo Iye ali. Tsopano, pa ulendo akupita. . .

47 Ndipo yang’anani, chinthu china, ngati ife tingati tiyankhule za ichi, changobwera mu malingaliro anga. Koma amuna anzeru omwe ankatsatira Nyenyezi, njira yonse kuchokera ku India, Kummawa, miyezi, akubwera kudutsa mu zigwa ndi zipululu, ankadutsa nyumba zoyang’anira mmwamba. Ndipo iwo ankasunga nthawi ya usiku ndi nyenyezi. Ndipo palibe wazambiriyakale kapena aliyense anayamba watchulapo za kuti anaiwona Nyenyezi iyo konse koma amuna anzeruwo. Iyo inali yoti iwo okha ayiwone Iyo.

48 Kotero inu mukhoza kuwona zinthu zomwe munthu wina sangakhoze kuziwona. Kwa iwe, Icho ndi chenicheni. Kwa iye, iwo samazimvetsetsa. Ziri ngati kutembenuka mtima; iwe ukhoza kutembenuzidwa ndi kumasangalala ndi madalitso a Mulungu, basi—kumangomwelela mu madalitso a Mulungu. Ndipo munthu winayo, atakhala pafupi ndi iwe, “Ine sindikuwonapo kanthu.” Mukuona? Mukuona? Ndi zimenezo. “Ine basi sindikuzimvetsetsa izo. Ine sindikuwona chomwe chiri cha izo zonse.” Chabwino, iye basi sakumvetsetsa Izo. Ndizo zonse. Pomwe, inu muli.

49 Zindikirani tsopano, Paulo ali paulendo wake akupita. Ndipo mwamsanga pamene chomuchitikira chachikulu ichi chinachitika kwa iye. . . Tsopano, iye sanali wokhutitsidwa. . . Ndi chimene chimamupanga Paulo kukhala wabwino kwambiri, tsopano.

50 Phunziro lathu usikuuno si lakuya. Ilo ndi phunziro losaya, koma, o, ife tifika mwakuyamo, pakapita kanthawi. Koma ili ndi phunziro losaya kwambiri, koma uku ndi kungoyambapo. Ndipo chomwe ilo liri, ndi chinthu chimodzi, ndicho kumukweza Yesu Khristu. Paulo, pakuyamba nazo.

51 Ndipo iye asanachite izi, Paulo anali sikolala wa Baibulo. Ndipo sikolala wa Baibulo sangasamilitse chiphunzitso chake pa zomuchitikira. Ayi, bwana. Iwo sadzasamilitsa konse chiphunzitso chawo pa chowachitikira. Inu mukhoza kukhala ndi mtundu uliwonse wa chokuchitikirani. Koma icho chiyenera kukhala chiri PAKUTI ATERO AMBUYE. Kulondola.

52 Tsopano, mu Chipangano Chakale, anali nazo njira zitatatu zosiyana zomwe iwo ankadziwira uthenga. Yoyamba, lamulo, ilo linali lamulo basi. Kenako, iwo anali naye—mneneri; wolota; ndipo iwo anali nayo Urimu ndi Tumimu. Tsopano izo zikhoza kukhala zakuya pang’ono.

53 Urimu Tumimu inali chapachifuwa chomwe Aroni ankavala pa chifuwa chake. Mmenemo munali miyala thwelofu: yaspi, sardio, kalbankulo, ndi ina yotero, mpaka pansu. Iwo ali nayo yonse miyala thwelofu yaikuluyo, yomwe inali mu chapachifuwa, kusonyeza kuti iye anali wansembe wamkulu wa fuko lirilonse, mafuko thwelofu a Israeli. Chapachifuwa ichi chinkapachikidwa pa nsanamira mu mpingo. Ndipo pamene mneneri alosera, ndipo iwo akafuna kutsimikiza kuti zinali zolondola, kapena ayi. Aneneri kapena olota ankaima pamaso pa Urimu Tumimu iyi, ndipo iye ankanena maloto ake kapena masomphenya ake, chirichonse chomwe iye anali atachiwona. Ndipo ngati Kuwala Kopatulikako. . . O, kodi inu mukuziwona izo? Mulungu nthawizonse wakhala mu malo azauzimu. Kuundana, kuwala uko, kunali kozoloweleka mpaka liwu ili litayankhulidwapo. Ndipo pamene liwulo linkakhudza miyala iyo, ngati izo sizinali zauzimu, icho chinkangokhala

matalala. Koma ngati izo zinali zauzimu, Kuwala uko konse kunkanyezimiritsa mitundu ya utawaleza palimodzi. Amen. Ndiye, uyo anali Mulungu akuyankhula, “Uyo ndi mneneri Wanga. Loto ilo lachokera kwa Ine.” Izo zinali molingana ndi Urimu Tumimu momwe iwo ankaweruzira.

54 Mukukumbukira Saulo pamene iye anabwerera mmbuyo? Iye anati sankatha kulota loto. Ndipo mneneri, Samuele, anali atafa, ndipo panali popanda njira. Iye anati, “Ngakhale Urimu siikukhoza ngakhale kuyankhula kwa ine.” Palibe. Saulo anaima pamaso pa Urimu, ndipo mawu ake anali okufa zanzi. Mukuona? Mulungu ankangomukana iye. Ndipo Urimu Tumimu iyo, iyo inali chitsimikiziro cha unsembe wa Aroni. Pambuyo pa kupita kwa Aroni, Mose . . . M—mbaleyo inkapachikidwa pa nsanamira.

55 Tsopano, unsembe wa Aroni unatha pamene Yesu anafa. Ndipo tsopano, analekanitsa lamulo kwa chisomo, ife tiri nayobe Urimu Tumimu. Ndipo Paulo ankaigwiritsa ntchito Iyo. Mukuona? Urimu Tumimu lero ndi Mawu a Mulungu Achisavundi, Amuyaya, osatha. Mukuona?

56 “Pakuti aliyense yemwe ati adzachotsere chirichonse kuchokera mu Bukhu ili, kapena kuwonjezera chirichonse kwa Ilo.” Ine sindikufuna chirichonse kunjira kwa Ilo, koma ine ndikufuna zonse zomwe Ilo liri nazo. Uwo ndi Mpingo womwe ife tikuufuna. Ndipo zinthu zonse ziyenera kuti zizitsimikiziridwa ndi Mawu.

57 Ndicho chifukwa ine ndinatenga kulephera posachedwapa pakati pa anthu Achipentekoste, chifukwa, chakuti, “Ine sindinkatha kumvetsa pamene mafuta ati ayenderere kuchokera mmanja mwako, kapena magazi kuchokera pa nkhope yako, nkumati chinali chizindikiro cha kuti unali ndi Mzimu Woyera.” Izo siziri Mwamalemba ndipo i—ine sindikanakhoza basi kuzitenga izo. Izo ziyenera kuti zizibwera kuchokera mu Mawu.

58 Ndipo tsopano, Paulo, iye ankangowakonda Mawu. Chotero, iye asanachitire konse umboni chomuchitikira chachikulu ichi chimene iye anali nacho, iye anapita umo mu Igupto kwa zaka zitatu. Ine ndikukhulupirira izo zinali zaka zitatu, zaka zitatu ali umo mu Igupto. Ndipo inu mukudziwa chimene ine ndikukhulupirira kuti iye anachita? Ine ndikukhulupirira kuti iye anatenga Chipangano Chakale, ndipo anafufuza kudutsa mu Chipangano Chakale, ndipo anapeza kuti Uyo anali kwenikweni Mesiya mwamtheradi. Iye ankayenera kukatsimikizira chomuchitikira chake mwa Baibulo. Amen. O, mai!

59 Tayang’anani pa iye pamene iye anali mu ndende. Inu mukuzindikira, panali—danga la moyo wa Paulo pamene iye anali mu ndende uko kwa nthawi yaitali. Iye analemba Bukhu la Aefeso. Iye analemba Kalata ya Ahebri iyi. Mukuona? Iye anali nayo nthawi. Mulungu anakamuika iye kutali uko mu

ndende, ndipo iye analemba Makalata awa kwa mipingo. Ina kwa mpingo waku Efeso. Iye analemba ina kwa mpingo wa Chipentekoste, anali ndi zovuta zambiri ndi iwo. Mpingo wa Chipentekoste iye anali ndi mavuto ochuluka nawo kuposa wina uliwonse. Tikadali nawobe iwo. Koma iye anali wothokoza kwambiri chifukwa cha iwo. Chinthu chokha chomwe iye akanakhoza kuwaphunzitsa iwo... Pamene iwo abwera umo: wina anali ndi lirime, wina anali ndi salmo, wina anali ndi kutengeka, wina anali ndi kumvera. Iye sakanakhoza kunena, kuyankhula kwa iwo, "Chitetezero chamuyaya." Iye sakanakhoza kuyankhula ndi iwo, "kukonzedweratu." Iye sakanakhoza kuyankhula kwa... Iwo anali makanda. Iwo onse ankayenera ku—ankayenera kuti amverere chinachake, kapena kuwona chinachake, kapena kukhala ndi kumvera kwachilendo, ndi, kapena chinachake pozungulira iwo, maumboni ena.

⁶⁰ Koma ine ndikukhulupirira, pamene iye ankayankhula kwa Aefeso, iye ankakhoza kuyankhula pa, "Mulungu anatikonzeratu ife kuti tikhale ana aamuna ndi aakazi, ndipo anatitenga ife ngati ana ake mwa Yesu Khristu asanaikidwe maziko a dziko." Tayang'anani pa izo. Mai!

⁶¹ Muwoneni iye akubwera mu Bukhu la Aroma, ndi ena otero. Iwo anali aakulu usinkhu. O, iwo ankayankhula ndi malirime, zedi, ndipo iwo anali ndi zizindikiro zina za Mzimu Woyera pakati pawo. Koma iwo sankapanga tiziphunzitsa, ndi zotengeka, ndi kunjenjemera pang'ono, ndi kumvera kwachilendo.

⁶² Paulo anati, "I—i—inū mukupita mowonjeza ndi izo. Pamene inu nonse mukuyenera kuti muziphunzitsa, inu mukadali makanda ndipo mukuyenera kuti muzikhala ndi mkaka."

⁶³ Ndipo icho ndi chimene ine nthawizonse ndayesera kuti ndilimbanire naye kachisi uyu kuti akhale, osati gulu la makanda. Tiyeni tikhale okula msinkhu. Imani pa msewuwo. O, mai! Ndi inu apo.

⁶⁴ Kotero, Paulo akupita kumusi uko, choyamba, kuti akawone ngati chomuchitikira chake chikufanana ndi Baibulo la Mulungu.

⁶⁵ O, kodi izo sizikanakhala zodabwitsa, lero, ngati anthu akanangochita izo kachiwiri, ngati ife tikanapanga chotichitikira chathu kufanana ndi Baibulo la Mulungu? Ngati icho sichingatero, ndiye chotichitikira chathu ndi cholakwika; icho sichikuwalira mu Urimu Tumimu. Ngati icho chikuwalira mkati Mmenemo, ameni, ife tachipeza Icho. Koma ngati icho sichiri, mwina... Ine sindikusamala momwe izo zikuwonekera zabwino, momwe kwenikweni izo zikuwonekera ngati kuti izo zinali zolondola; ngati kuwala uko sikunawalire pa Urimu Tumimu iyo, izo zinali zolakwika.

⁶⁶ Ndipo ziribe kanthu kuchuluka kwa zokuchitikirani zomwe inu mwakhalapo nazo, momwe izo zikuwoneka kuti ndi zenizeni, momwe izo ziri zoperekeka, momwe izo zinaliri zamaphunziro, chida chachikulu chomwe chiri chopindulira miyoyo; ngati icho sichikuwalira mu Mawu, icho ndi cholakwika. Kulondola. Izo ziyenera kumafola limodzi ndi Mawu.

⁶⁷ Tsopano, ine ndikukhulupirira, ndipo pali pakati pa msewu. Msewu, tsopano, nthawi zambiri. . . Ine ndinkakonda kupita ku mpingo wa Nazereni. Ambuye awadalitse anthu okondeka awo. Amethodisti akachitidwe-kachikale, oyeretsedwa ndi chomwe iwo ali; mpingo wa Mulungu, Anazereni, a Pilgrim Holiness, ndi ambiri a mipingo yabwino ya chiyeero iyo. Ndipo iwo anakakonda kuimba nyimbo:

Ine ndikuyenda mu msewu waukulu wakale,
Ndikuwauza kulikonse komwe ine ndikupita,
Kulibwino ine ndikhale Mkristu wachikale,
Ambuye,
Kuposa chirichonse chomwe ine
ndikuchidziwa.

⁶⁸ Zabwino. Zodabwitsa. Ndiyeno iwo anakakonda kunena za msewu wawukulu wa chiyeero. Tsopano, ngati inu mungawerenge izo mobwereza, iwo akuzitenga izo kuchokera pa Yesaya, mutu wa 35. Tsopano, ngati inu mungazindikire, iye anati, “Padzakhala pali msewuwaukulu, *ndi njira*.”

⁶⁹ Tsopano, *ndi* ali cholumikizira. Mukuona? Msewuwaukulu, iwo sunali msewuwaukulu wa chiyeero. “Kudzakhala kuli msewuwaukulu, *ndi njira*, ndipo iyo izidzatchedwa, ‘Njira ya chiyeero,’” osati msewu waukulu wa chiyeero. “Njira ya chiyeero!” Ndipo njira ya msewu imakhala pakati pa msewu. Iwo umamangidwa monga *chonchi* chotero kuti madzi azikokololera zinyansi, ku mbali zonse ziwiri, kuti msewuwo uzikhala waukhondo. Inu osatero, inu muzikhala ndi zithaphwi ziri mu msewu wanu, nthawizonse, ngati iwo sunamangidwe moyenera. “Njira” ili pakati pa msewu.

⁷⁰ Tsopano, ku mbali *iyi*, pamene anthu atembenuka, malingaliro awo amakhazikika pa Khristu pomwe. Ndipo ngati iwo ali ophunzira pang’ono pokha, ndi kusamakhalabe pansu pa pemphero, iwo amafika pozizira kwenikweni, ndi kuwuma, ndi kukhuthara, ndi kusayanjanitsika. Ndiyeno ngati iwo angokhala amanjenje pang’ono, ngati inu simusamala, iwo amangofika amakani ndi olusa, ku mbali *iyi*, mwaona, iwo amapita mu zomverera ndi chirichonse.

⁷¹ Tsopano, koma, Mpingo weniweni ndi Uthenga waubwino weniweni, pakati pa msewu pomwe. Iwo si wozizira ndi wokhuthara, ngakhalenso iwo si wotentheka. Iwo ndi Uthenga weniweni wabwino, wachikale, wofunda, wa chikondi cha Mulungu chomvereredwa mu mtima, chikupita mmusi momwe

pakati pa msewu, ukuitanira kuchokera ku mbali zonse. Ndiko kulondola. Tsopano icho ndi chimene. . . Ndipo kodi inu mungazipeze motani izo, mpingo? Kuchokera mu Mawu momwe, Urimu Tumimu.

⁷² Tsopano, Paulo ankafuna kuti awutengere mpingo uwu pakati pa msewu pomwe, kotero iye anapita nakaphunzira zaka zitatu pa Malemba omwe iye ankawadziwa. Chotero, Paulo analemba gawo lalikulu la Chipangano Chatsopano ili. Mulungu anampangitsa iye kuti achite izo chifukwa cha kubwera kwa m’badwo wa Amitundu uwu. Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, Mauthenga anai, iwo anali Ayuda. Koma Paulo analemba ochuluka a makalatawo.

⁷³ Tsopano zindikirani, tsopano, ife tikuti tiyambe kupeza maziko awa tsopano, komwe iye ali, akulemba Iwo, kuchokera ku ndende. Ndipo iye anali nacho chomuchitikira chonse ichi. Koma, poyamba, chomuchitikira ichi poyamba chinatsimikiziridwa, ndipo iyi ndi kalata yake ya fungulo kwa izo. Iyi ndi kalata yake ya fungulo. Aroma ndi Aefeso, ndi ena otero, ali nawo malo awo, koma iyi ndi kalata ya fungulo.

⁷⁴ Tsopano, mutu wonse wa 1, uli, kumukweza Yesu, ndi kumulekanitsa Iye kuchokera pa kukhala mneneri. Ndicho cholinga chonse tsopano. Ine ndiyesera kuti ndifike ku izo mofulumira basi momwe ndingathere tsopano, chotero kuti ife tisakhale motalika kwambiri. Cholinga chonse, kuli, kulekanitsa mutu watsopano. . . watso. . . Mutu wa 1, uli, kumulekanitsa Yesu kwa mneneri aliyense, kapena lamulo lililonse, kapena zina zotero, ndi kusonyeza Yemwe Yesu ali. Tsopano penyani, “Mulungu.” Ife tikuyambapo, mawu oyamba, “Mulungu.”

Mulungu, pa dzuw-. . . yemwe pa nthawi zamakedzana. . .

Zamakedzana akutanthauza kuti “kutali mmbuyo,” nthawi zammbuyo.

. . . nthawi zamakedzana ndi mkachitidwe kosiyanasiyana ankayankhula kalelo kwa makolo athu mwa aneneri,

⁷⁵ Tsopano, onani, “Mulungu, mu nthawi zakamakedzana, kutali mmbuyo, Iye ankayankhula kwa makolo athu mwa aneneri.” Umo ndi momwe Iye anali kuperekerwa Uthenga Wake, kudzera mwa mneneri Wake.

⁷⁶ Mulungu ankakhoza kutumiza mneneri Wake monga Eliya, Yeremiya, Yesaya. Ndipo ngati inu mungazindikire, palibe mu mbiriyakale yonse ya mdziko, pomwe mpingo unayamba wabala mneneri. Fufuzani izo mu Chipangano Chakale, Chipangano Chatsopano, kapena mu tsiku lino, mu tsiku lotsirizali. Ndisonyezeni ine mneneri aliyense yemwe anayamba waledwapo kuchokera mu mpingo mu tsiku lotsiriza. Ndisonyezeni ine mmodzi yemwe anayamba

watulukapo, kunja. Ndipo ndisonyezeni ine nthawi imodzi yomwe mneneri, wantchito weniweni wa Mulungu, yemwe kachitidwe kachipembedzo ka mdziko sikanamutsutse iye.

⁷⁷ Tangoganizani za izo. Yeremia, Yesaya, onse kutsika kudutsa mu Chipangano Chakale, iwo amazitsutsa izo. Yesu anati, “Inu mumakongoletsa manda a aneneri ndi kuwapanga iwo kukhala ojera, ndipo inu munawaika iwo mmenemo.” Ndiko kulondola.

⁷⁸ Mpingo ukupitiriza zimenezo. Tayang’anani pa Patrick Woyera. Inu anthu Achikatolika mumadzitengera iye. Iye si wa Chikatolika kuposa momwe ine ndiriri. Ndiko kulondola. Koma inu mumadzitengera iye.

⁷⁹ Yang’anani pa Francis Woyera waku Assisi. Mumadzitengera iye. Iye si wa Chikatolika kuposa momwe ine ndiriri.

⁸⁰ Yang’anani pa Joan waku Arc. Inu munamuwotcha iye pa nkhuni, monga mfiti, chifukwa iye ankawona masomphenya ndipo anali wauzimu. Munamuwotcha iye pa nkhuni. Ndipo mkazi uyo akufuulira chifundo, ndipo iwo anamuwotcha iye pa nkhuni. Pafupi zaka handiredi kenako, iwo anadzapeza kuti iye anali mneneri wamkazi. Iye anali wantchito wa Mulungu. O, ndithudi, inu muli ndi chilango chachikulu: inu munafukula matupi a ansembe ndipo munawaponyera iwo mu mtsinje.

⁸¹ “Inu mumakongoletsa manda a aneneri, ndipo munawaika iwo mmenemo.” Kulondola. Palibe pomwe kachitidwe kachipembedzo kanayamba kabalapo munthu wa Mulungu; palibe pomwe anatero, sizinatero lero, ndipo sizidzatero konse. Chipembedzo chopangidwa bungwe sichinayambe chakhala cholinga cha Mulungu.

⁸² Mpingo wakale kwambiri wabungwe mu dziko ndi mpingo wa Katolika; Lutera, kachiwiri; ndiye anabwera Zwingli; pambuyo pa Zwingli, anabwera Kalvini; Kalvini, kupitirira, Achianglikani, Angelezi Achisaxoni, kenako mpingo wa Anglikani; ndi King Henry wa Chisanu ndi chitatu, pamene iye anatsutsa, ndi zina zotero; ndi kupitirira mmusi kwa Methodisti ya Wesley, ndi Nazareni, Pilgrim Holiness; ndi kupitirira mmusi kwa wotsiriza, ndiye Achipentekoste, onse anapanga bungwe. Ndipo Baibulo mophweka limaphunzitsa kuti mpingo wa Katolika ndi—mkazi wa mbiriyoyipa, ndipo mipingo ya Chiprotestanti ndi mabungwe awo ili ana aakazi ake, Chivumbulutso 17. Ndizo ndendende kulondola. Kotero iwo ali . . .

⁸³ Osati anthuwo, tsopano. Muli abwino mu mipingo yonse iyo; anthu oyeretsedwa, opulumutsidwa. Koma Mulungu samaitana anthu Ake mwa bungwe. Iye amawaitana iwo mwa pawekha. Mulungu amachita nawe payekha, kaya ndiwe wa Chimethodisti, Chibaptisti, Chiprotestanti, ndi Chikatolika, kapena chomwe iwe uli. Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko, anakudziwani inu, ndipo anakukonzeketseranitu inu ku Moyo

Wamuyaya, kapena mwina inu munakonzeketseredweratu ku kutaika Kwamuyaya. Osati. . .

⁸⁴ Iye sanali kulolera kuti inu muwonongeke, inu mukanati mudzawonongeke. Koma, Iye pokhala wopandalalire, Iye ankayenera kuti azidziwa mapeto kuchokera kuchiyambi, kapena Iye si Mulungu. Kotero Yesu sanangobwera ku dziko lapansi kuti adzangoti, “Chabwino, ine ndiwona ngati winawake akhala wachifundo. . . Ngati ine nditi ndichitepo ndi kufa, mwa njira yovuta, iwo mwina azidzaganiza, ‘Chabwino, ine. . .’ Izo zidza—izo zidzaiakamiza mitima yawo, ndipo iwo adza. . .” Mulungu samayendetsa ntchito Yake monga choncho.

⁸⁵ Yesu anadzera cholinga chimodzi chodziwika, ndicho, kuti adzawapulutse iwo omwe Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko, ankadziwa kuti akanati adzapulumutsidwe. Iye ananena chomwecho. Ndiko kulondola. Kotero inu. . . “Si iye yemwe afuna, kapena iye yemwe athamanga; ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.” Paulo ananena zimenezo. Munthu yemweyo apa.

⁸⁶ Iye anati, “Ndicho chifukwa Mulungu akanakhoza kunena kuti, Esau kapena Yakobo asanabadwe nkomwe, Iye anati, ‘Ine ndinamkonda mmodzi ndi kumuda winayo.’” Asanabadwe wina wa anyamatawo, Mulungu ankadziwa kuti Esau anali shasha, ndipo Iye ankadziwa kuti Yakobo anali. . . iye ankakonda ufulu wakubadwa wake. Kotero Iye anadziwa, dziko lisanawumbidwe nkomwe, za izo. Tsopano, ife tikuti tipeze mu miniti Yemwe uyo anali yemwe ankadziwa izo. Mutu uwu uli nazo izo.

Mulungu, . . . mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyana ankayankhula. . . kwa makolo athu mwa aneneri,

Mmasiku otsiriza ano wayankhula kwa ife mwa Mwana wake, . . .

Wachita chiani? “Wayankhula kwa ife mu masiku otsiriza ano mwa Mwana Wake.”

⁸⁷ Tsopano, inu mukanaganiza chotani ndiye, kuti, kodi mneneri akanakhala chiani? Kodi ife tikanakhala ndi mneneri ndiye wa tsiku lino? Mwamtheradi. Kodi Iye akanamayankhula mwa iye? Zedi. Koma iye amene. . . Aneneri a masiku akale anali Mzimu wa Yesu Khristu.

⁸⁸ Tsopano, tiyeni tizitenge mowongoka, chifukwa ine sindikuganiza kuti izo zikulowerera moyenera. Tsopano, izi ziri ngati Sande Sukulu, kotero ife tikufuna kuti tizitenge izi momveka. Mukuona?

⁸⁹ Zindikirani. Tiyeni titenge Mzimu wa Mulungu umene unali mwa Mose, mwangwiro. . . ndi mthunzi wotsogolera wa Yesu Khristu. Ochitapo onse a Chipangano Chakale ankachita mthunzi motsogolera mtanda. Mose, anabadwa

mwana woyenera, anabisidwa mu mantcheza, anachotsedwa kwa makolo ake, zina zotero, ndipo anali. . . Iye anali mfumu, kapena—mtsogoleri, wopereka lamulo, wokhalira pakati, wansembe. Chirichonse chomwe iye anali chinkachita mthunzi motsogolera Khristu.

⁹⁰ Tayang’anani pa Yosefe, wokonedwa ndi abambo ake, wodedwa ndi abale ake, ndipo anagulitsidwa kwa pafupi zidutswa makumi atatu za siliva. Anaponyedwa mu dzenje, analingaliridwa kuti wafa; anachotsedwamo. Mu kuzunzidwa kwake, wophika mkate anapulumutsidwa, ndipo woperekerera chikho anataika; mbala ziwiri za pa mtanda. Ndiyeno pamene iye anatulukamo, iye anatuluka kuchokera mu dzenje ilo, ndipo anakhalitsidwa pa dzanja lamanja la Farao, kochitira malonda kwakukulu. . . f—f—fuko lomwe linakwapula dziko lina lonse. Ndipo palibe munthu yemwe akanakhoza kubwera kwa Farao kupatula iwo atabwera kudzera mwa Yosefe; Yesu kukhala pa dzanja lamanja la Mulungu, ndipo palibe munthu akanakhoza kudza kwa Mulungu kupatula kudzera mwa Khristu. Ndipo pamene Yosefe ankachoka pa mpando uwo nayamba kutuluka, amuna ankapita patsogolo pa iye, akufuula ndi kuwomba malipenga, akumveketsa lipenga, kuti, “Gwaditsani bondo! Yosefe akubwera.”

⁹¹ Ndipo pamene Yesu akubwera, lipenga lidzomba, ndipo bondo lililonse lidzagwada, ndi lirime lililonse lidzavomereza. Inde, bwana. Apo Iye anali.

⁹² Ndipo pamene Yosefe anafa, iye anasiya chikumbutso kwa iwo omwe anali kuyembekezera chiwombolo.

⁹³ Ine ndinaika dzanja langa pa bokosi lamaliro lakalelo, kuno osati kale litali, ilo linapangidwa ndi nkala. Ndipo thupi lake linkayenera kuti likhalepo. . . mafupa ake. . . Anati, “Musati mudzandiike ine kuno, chifukwa tsiku lina, Mulungu adzakuchezerani inu.” Iye anali mneneri. “Mulungu adzakuchezerani inu.” Ndipo anati, “Pamene inu muzidzapita ku dziko lolonjezedwalo, mudzatenge mafupa anga.”

⁹⁴ Uko, wa Chihebri wokalamba, ali ndi nsana wokwapulidwa ndi wamagazi, ankakhoza kuyang’ana mu bokosi lamalirolo nkumati, “Tsiku lina, ife tidzatulukako kuno.”

⁹⁵ Yesu anasiya chikumbutso, manda apululu. Tsiku lina pamene ife titi tidzapite kumanda, ndi okonedwa athu, ndi kudzatimva timabulumu ito, pamene iwo azidzati, “Phulusa ku phulusa, ndi fumbi ku fumbi, ndi dothi ku dothi.” Koma, m’bale, ife tikhoza kuyang’ana kutsidya kwa nyanja, ku manda apululu. Tsiku lina, ife tidzachokako kuno. Ife tikupita kwathu. Iye akubwera. Chirichonse chinaimiridwa.

⁹⁶ Tayang’anani pa Davide, wokanidwa ndi anthu ake omwe, anachotsedwa pa mpandowachifumu ndi anthu ake omwe. Pokhala mfumu ya Yerusalemu, anathamangitsidwa mu

Yerusalemu ndi anthu ake omwe. Ndipo pamene iye anali akukwera Phiri la Azitona, iye anayang'ana mmbuyo ndipo analira. Iye anali atakanidwa.

⁹⁷ Zaka mazana asanu ndi atatu kuchokera pamenepo, Mwana wa Davide, Mfumu ya Yerusalemu, anakhala pa phirilo ndipo analira, chifukwa iye anakanidwa.

⁹⁸ Umenewo unali Mzimu wa Khristu mwa Davide. Onse ankachitira mthunzi motsogolera mtanda. Aneneri amenewo kumbuyo uko ankayankhula mu Dzina Lake. Iwo ankakhala moyo mu Dzina Lake. Iwo ankachita mu Dzina Lake. Zedi. “Mulungu mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyana ankayankhula kwa makolo athu kudzera mwa aneneri, koma mu tsiku lotsiriza lino kudzera mwa Mwana Wake.”

⁹⁹ Koteri aneneri ndi amuna auzimu, tsiku lino, ali kokha chinyezimiritso cha Khristu. Apo, mwa lamulo iwo ankaima, onani. Cha kuno iwo akuima, akuyang'ana mmbuyo mbali inayo, kudzera mu chisomo.

¹⁰⁰ Izo mu Ahebri 11, mutu wotsiriza, ine nthawizonse ndakhala ndikudabwa zimenezo. Mu mutu wotsiriza, gawo lotsiriza la mutu wa 11 wa Ahebri, pamene iye akuyankhula za Abrahamu. Mutu waukulu wa chikhulupiriro, ndipo pa mapeto, iye anati, “Iwo ankayendayenda mu zikopa za nkhusa ndi mu zikopa za mbuzi, ndipo anapangidwa opanda pokhala ndipo ankang'ambidwa pakati. Iwo ankangoyendayenda, analibe malo oti apiteko, odanidwa, ndi onyozedwa, ndi ozunzidwa. Za omwe, dziko lino siliri loyenera anthu oterowo.”

¹⁰¹ Ndiye Paulo akuima nati, “Koma popanda ife iwo sali angwiro.” Pakuti iwo ankangoyang'ana *ku* mtanda, ndipo ife tikuyang'ana *kupyola* mu mtanda. Ife tiri nawo Mzimu wa Khristu Iwo utakhala kale mnofu wa munthu nudzakhala pakati pathu. Ife tinabwera kuno mwa Mzimu Woyera, lomwe liri dongosolo labwinopo mwapatali.

¹⁰² Ndipo nthawizina ine ndimadabwa chomwe Chikhristu chikuyembekeza lero. Mlaliki woyenda ndi chihema angasowe kuti akhale...kapena mpingo wina watsopano kapena ulamuliro wina watsopano, kumadzitcha yekha mneneri, amapita apo, nkuti, “Chabwino, ngati iwo ati andipatse ine ndalama zochuluka chomwechi. Ngati ine ndingakhale ndi galimoto yabwino kwambiri. Ngati iwo...Ngati malipiro anga ati azikwezedwa miyezi sikisi iliyonse.”

¹⁰³ Ife timayenera kumakhala ndi zapamwamba. Ife timayenera kumakhala ndi manyumba apamwamba. Ife timayenera kumakhala ndi zovala zapamwamba. Kodi ife tidzachita chiani pamene tidzaima pamaso pa amuna awo omwe ankayendayenda, mu zikopa za mbuzi ndi zikopa za nkhusa, alibe malo oti nkuikapo mitu yawo, anali kungoyendayenda mu zipululu? Ndipo winawake akatiseka ife timakhala okonzeka kuti tisiye

mpingo ndi kusabwereranso uko kenanso. Chomwe Chikhristu chikufuna lero. Ife tiyenera kuti tizidzichitira manyazi ifeeni.

O Mulungu, khalani ochuluka chifundo kwa ife.

¹⁰⁴ Mu tsiku ilo, Iye ankayankhula mwa aneneri, koma tsiku lino kudzera mwa Mwana Wake. Awo anali mawu a mneneri, uko. Awa ndi Mawu a Mwanayo, lero. O, lidalitsidwe Dzina la Ambuye!

¹⁰⁵ Mwa kuyankhula kwina, ngati inu mukuyang'ana pa mthunzi, choimira, inu mukhoza kulakwitsa. Koma Ichi ndi chotsukidwa, chithunzicho chikuwoneka bwinobwino. Izo zinali mwa aneneri; izi ndi mwa Mwana Wake. Izo zinali mwa choimira; ichi ndi mwa chenichenicho. Amen. Inu mukuziona izo? Apa palibe mwayi woluzira. Ndi chinthu chenicheni, tsiku lino kudzera mwa Mwana Wake. O, kudabwitsa kwakeko!

. . .yemwe iye anamuika kukhala wolandira . . .(O, mai) . . .wolandira zinthu zonse, . . .

¹⁰⁶ Kunali kutani uko? Uko kunali kuikidwa. O, mvetserani. Iye anaikidwa, Khristu anali, wolandira wa zinthu zonse. O, Mdierekezi amazidziwa zimenezo, kuyambira ku munda wa Edeni, inu mukuwona, pamene Mdierekezi anamva Mawu amenewo uko tsiku lija, pa chiweruzo cha anthu awo. Anati, “Chifukwa inu munachokera ku fumbi; ku fumbi inu mudzabwerera; ndipo Mbewu ya mkazi idzavulaza mutu wa serpenti.” Mbewu yolonjzedwa.

¹⁰⁷ Satana mowirikiza ankayang'ana kufuna Mbewu imeneyo. Pamene Abele anabadwa, iye anati, “Ndi iwe apo, ndi mbewu ija.” Ndipo iye anamupha Abele. Mwana Wake, Kaini, anamupha Abele. Ndipo mwamsanga pamene Abele anafa, iye anati, “Ine ndaip Ezeketa mbewu.” Iye anaipha iyo. Iye anati, “Ine ndathana nayo iyo.” Koma, imfa ya Abele, kubadwa kwa Seti kunali chiukitsiro kachiwiri. Penyani momwe iwo anabwerera mmusimo.

¹⁰⁸ Mzere wa Seti uwo, iwo unabwera mmusimo, anthu odzichepetsa, olungama; kupitirira mmusi kudutsa mwa Enoki; kupitirira mmusi kwa Nowa, mpaka kumathero a chiwonongeko cha chigumula.

¹⁰⁹ Tayang'anani pa mzere wa Kaini, anakhala anthu anzeru, ophunzira, asayansi. Kodi Baibulo silinanene . . .Kodi Yesu sananene, kuti, “Ana a dziko lino ndi anzerupo kuposa Ana a Ufumu”? Tayang'anani ku mbali ya Kaini ngakhale lero: anzeru, ophunzira, okaikira, achipembedzo kwambiri; onani, achipembedzo kwambiri, koma asayansi, omanga, amuna aakulu.

¹¹⁰ Atengeni amuna aakulu. Tayang'anani pa Thomas Edison, amuna ambiri otchuka. Tayang'anani pa Einstein, ubongo wa mdziko, otchedwa chomwecho, lero, ubongo wa mdziko.

Koma ife sitimayesera kugwiritsa ntchito ubongo. Ife timalola Malingaliro omwe anali mwa Khristu azikhala mwa ife, ndi kumayang'ana ku Mawu awa, ndi kudzitcha izo chomwecho.

¹¹¹ Adotolo azamankhwala, ngakhale ife timawapatsa iwo sawasha ndi chirichonse chomwe ife tiri nacho, koma ochuluka a iwo ndi okaikira, achikunja. Tayang'anani pa anthu anzeru, aluntha lero. Iwo ali ku mbali ina iyo uko, ku mbali ya Kaini.

¹¹² Koma tayang'anani pa odzichepetsa ndi ofatsa. Ndi icho chiukitsiro chanu kachiwiri. O, lidalitsidwe Dzina la Ambuye. Ndi inu apo. Zindikirani.

... iye anamupanga iye *kukhala wolandira zinthu zonse, mwa iye naponso iye anapanga maiko;*

Nndani anapanga maiko? Khristu. “Khristu anapanga maiko?” Inde, bwana. Tiyeni tingopita patsogolo pang'ono.

Yemwe pokhala chinyezimiro cha ulemerero wake, ndi maonekedwe enieni a kukhalapo kwake, . . .

Kuwala kwa ulemerero wa ndani? Ulemerero wa Mulungu. Maonekedwe enieni a Kukhalapo kwa Ndani? A Mulungu. O, ine ndikuzikonda izi!

... *kapena maonekedwe enieni a umunthu wake, ndi wogwirizira zinthu zonse mwa mawu. . .*

Ndi inu apo. Mawu, omwe amagwirizira zinthu zonse. Yesu ananena, mu Mateyu 24, “Miyamba ndi dziko zidzapita, koma Mawu anga sadzapita.” Iye akugwirizira zinthu zonse.

¹¹³ Sayansi ikuyesera kuziponderezera pansu Izo, ndi kuti, “Ndi Bukhu lakale. Ilo lakhala likumasuliridwa.”

¹¹⁴ Ngakhale mpingo wa Roma Katolika, Bishopu Sheen anati, “Ilo lakhala likumasuliridwa nthawi zinai kapena zisanu zosiyana, ndipo palibe zochuluka kwa Ilo. Inu simungakhoze kukhala moyo ndi Ilo ngati inu mukanati mutero.” Koma Iye amagwirizira zinthu zonse mwa Mawu Ake. Amen. Ndi chimene ine ndikuganiza za Ilo. Ine ndimakhulupirira Baibulo.

... *mawu a mphamvu yake, (muli mphamvu mu mawu), pamene iye anali mwa iyeyekha atachotsa machimo athu, . . . (yang'anani apa) . . . anakakhala pansu ku dzanja lamanja la Ufumu mmwamba;*

¹¹⁵ Kodi Paulo akuyesera kuchita chiani? Iye akuyesera kuti asonyeze kuti Mulungu analinga zinthu zonse mwa Khristu, ndipo Khristu anali maonekedwe enieni a Mulungu. Mutu wonsewo ukuchita ndi momwe kuti Iye anali wapamwamba kuposa Angelo, wapamwamba kuposa mphamvu zonse. Angelo ankamupembedza Iye. Paulo ankayesera kumukuza Iye.

¹¹⁶ Tsopano, ine ndikufuna kuti ndiyesere, ngati ine sindifika patali paliponse kuposa apa, zina zonse za izo ndi kungomukuza Khristu. Zimene Paulo akunena cha apa, monga mu mutu wa 11,

ndi zonse zokhudza kuyankhula za dziko. Iye anati, “Uti—Ndi Mngelo uti yemwe Iye anati, ‘Iwe ndi Mwana Wanga, tsiku lino ine ndakubala Iwe?’” Mukuona?

¹¹⁷ “Kutha kwa dziko, iwo adzawonongeka. Dziko lidzawonongeka. Koma...Ndipo zinthu zonse za mdziko zidzawonongeka. Iye adzazinyamulira izo mmwamba ngati chovala. Ilo lidzakhala litakalamba, ndipo lidzatembenuzidwa, ndi kuchokapo. ‘Koma Iwe ukhalapobe. Iwe ukhalapobe kwanthawizonse. Iwe ndi Mwana Wanga. Tsiku ili ine ndakubala Iwe, ndipo sudzawonongeka konse, utakhala pa dzanja lamanja la Ufumu.’”

Kodi *dzanja lamanja* limatanthauza chiani? Osati, kuti Mulungu ali ndi dzanja lamanja lomwe winawake wakhala pa ilo. *Dzanja lamanja* limatanthauza “mphamvu ndi ulamuliro,” ali ndi ulamuliro wa chirichonse Kumwamba ndi padziko lapansi. Ndipo Miyamba yonse ndi dziko lapansi zinapangidwa ndi Iye.

¹¹⁸ Tsopano, Mwamuna wamkulu Uyu ndi ndani, Munthu wamkulu uyu? Khristu. Apa, Mulungu mu Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, si... Ndi utatu, koma Iwo si utatu wa anthu. Ndi utatu wa udindo, wa Mulungu mmodzi.

¹¹⁹ Iye anali Atate akutsogolera ana a Israeli. Uwo unali udindo Wake, Yehova wamkulu Atate. Ndipo Iye anakhala pa dziko lapansi, akutchedwa Mwana. Ndipo tsopano Iye akukhala mu Mpingo Wake, akutchedwa Mzimu Woyera. Osati Amulungu atatu; Mulungu mmodzi mu maudindo atatu: Atate, Mwana, Mzimu Woyera.

Anthu amayesera kumupanga Iye Amulungu atatu osiyana, Mulungu Atate. Ndi chifukwa, Ayuda, inu simungakhoze konse... Inu simungabwerese konse izi kwa Myuda, ayi, izo uko. Iye sangakhoze. Iye ali nalo lamulo, kuti, “Ine ndine Mulungu Mmodzi.” Pali Mulungu mmodzi yekha.

¹²⁰ Mu Afrika iwo amabatiza njira zitatu zosiyana: iwo amabatiza kamodzi kwa Atate, ndi kamodzi kwa Mwana, ndi kamodzi kwa Mzimu Woyera. Apostolic Faith Mission, iwo amabatiza nthawi zitatu, chafufu mimba, kwa imfa Yake. Chimene iwo amachitcha Uthenga Wathunthu ku Chigwa Chakumadzulo, kapena Chigwa Chakummawa, amabatiza katatu chammbuyo, anatero Iye...kwa kuikidwa mmanda Kwake.

Ndipo iye anati, “Pamene Iye anafa, Iye anagwera chamtsogolo.”

¹²¹ Wina anati, “Dikirani. Inu mumamuika munthu mmanda chagada.” Basi tinthu takachitidwe tating’ono ito, pamene, iwo onsewo akulakwitsa; onse akulakwitsa, malingana ndi Lemba.

Iyi ndi Urimu Tumimu. Iyo imakhazikitsa izo.

¹²² Tsopano, apa, tiyeni tingojambula izo ndi kuwona chimene—momwe izo zikuwonekera, usikuuno. Ndi izi apa, ngati inu mukufuna kuti muziwone izo. Mu zaka zonse za pafupi twentefaii ine ndakhala ndiri mtumiki. Ine ndaziphunzira izo. Ndipo kawirikawiri ine ndakhala ndikudabwa pa mphatso za mu mpingo. Kodi mphatso zimenezo ndi chiani? Ulosi, kuyankhula ndi malirime, kutanthauzira kwa malirime, vumbulutso Laumulungu, zina zotero, zonsezo zimabwera kudzera mwa Khristu.

¹²³ Tsopano penyani. Khristu ndi Mutu wa zinthu zonse. Ndipo iye ndi Mutu wa Mpingo. Ndipo kodi inu munayamba mwaiwonapo daimondi yaikulu? Daimondi yaikulu yomwe yadulidwa moyenera, ili ndi timabanthu tating'ono titabanthulidwa pa iye, kubanthulidwa pa iye. Izo zimapanga daimondi yoyenera. Kodi tizibanthuto ndi tachiani? Daimondi yeniyeni, yomwe iyo imatulukira, iyo imakhala itavulazidwa; daimondi yeniyeni, pamene iyo yapezedwa.

Ine ndinali mu Kimberly. Inu, ambiri a inu, omwe munamvapo kuti iwe ukhoza kutola daimondi pa msewu, uko nkulondola. Billy ndi ine, ndi Bambo Bosworth. Apurezidenti a migodi ya daimondi ku Kimberly, kutenga. . . Iye anali wondithandizira wanga mu msonkhano kumeneko. Ndipo iwo anatitengera ife uko. Ndipo kunjira kokha kwa. . . Iwo amaifukula iyo, o, pafupi mapazi seventini handiredi pansu pa dziko. Iyo imatuluka ili, mwala wa buluu, wabuluu waukulu, monga mwala wa buluu uwu umene inu mumawupeza cha kuno. Ndipo mbadwa izo, iwo amaziika izo mapazi seventini handiredi awo pansu, kuti amukumbe iye, kuti mtengo uzikhala wokwera. Inu mukhoza kupita ku mtsinje uko, iwo amawutetezera iwo kwa mailosi mahandiredi. Kutenga zibekete ziwiri za magaloni-khumi, iye anati, ndi kuzinyamula izo, zodzaza n—ndi mchenga, ndipo ngati iwe ungakafike kwanu ndi izo, iwe ungakhale wamamilioni ambiri, mungakhale muli daimondi wambiri chotero mmenemo. Koma iwo amayenera kugwira ntchito ndi kumukumba iye, kuti asunge mtengo wokwera wa iye.

¹²⁴ Tsopano, daimondi, pamene iyo ikubwera apo, iyo imakhala chidutswa chachikulu basi, chosalala, chobulungira monga chidutswa chagalasi. Pali daimondi ya buluu, daimondi, yakuda, ambara, ndi daimondi yowonekera, daimondi yoyera. Koma pamene iyo imabwera apo. . . Ndiye pamene iyo yapangidwa kuikidwa kogwiritsidwa ntchito, pali gawo la daimondi imeneyo yomwe iyenera kutaidwa. Ndipo iyo imayenera kuti itaye—zibanthu za iyo. Kuwaza tizibanthu tating'ono, chifukwa, pamene iyo ibwera mu kuwala kolunjika, monga *chomwecho*, iyo imapangitsa kunyezimira. Chibanthu, nchomwe chimapangitsa kuthwanima, momwe iyo imadulidwira. Iyo imadulidwa, imawazidwa, ndiyeno, pamene iyo itero, iyo imapangitsa kuthwanima. Ndipo wina kumakhala kuwala kobiliwira, kwina

kumapita kukuwala mwa buluu, ndipo mwinamwake kwina, kuwala kwa ambara, ndi kuwala kofiira. Ndipo kuwala kosiyana kumapita kuchokera kwa iyo, monga kuwala kwa utawaleza. Iwo amazitcha izo, “moto wa mu daimondi.”

¹²⁵ Tsopano, kulikonse kwa kuwala uko kumaimira mphatso. Koma ndi, Khristu yekha ali Daimondi. Ndipo Iye anali Mmodzi Yemwe anabwera, ndipo anatunduzidwa, ndipo anavulazidwa, ndi kugwazidwa, kuti Iye akhoze kudziyenezimiritsa Yekha monga Kuwala kwa dziko. Iye ndi Bwana Daimondi monga uja.

¹²⁶ Kodi inu mungalingalire, kusanakhale konse dziko lapansi, kusanakhale konse kuwala, kusanakhale konse nyenyezi, kusanakhale konse chirichonse? Kunali Kasupe Wamkulu akuyenda uko, wa Mzimu, ndipo kuchokera mu Kasupe uyu munatuluka chikondi changwiwo kwambiri, chifukwa kunalibe kwina komwe icho zikanachokerako koma ku chikondi icho. Tsopano, ife, chimene ife timachitcha chikondi, lero, ndi chikondi chopotozedwa. Koma basi pamene ife tiri ndi nnunkhira, kapena pang’ono pokha pa chikondi icho mwa ife, icho chimasintha lingaliro lathu lonse.

¹²⁷ Ndiye kuchokera mmenemo kunabwera mtsinje wina, kuchokera ku Kasupe wamkulu uyu, Daimondi, ndipo iye ankatchedwa chilungamo, chilungamo mwamtheradi. Tsopano, ndicho chifukwa ife tinkayenera kuti tikhale ndi lamulo. Ndicho chifukwa lamulo linkayenera kukhala ndi chiweruzo. Ngati palibe chiweruzo chisakutsatira lamulo, lamulo silichita ubwino ayi. Ndipo pamene chiweruzo chinaperekedwa ndi lamulo, lomwe chimabweretsa imfa, ndipo panalibe wina yemwe akanakhoza kulipira dipo koma Mulungu Mwiniwake. Ndipo Iye analipira dipo la imfa yathu, ndipo anatenga machimo athu pa Iye, kuti ife tikhoze kumakhala chilungamo cha Mulungu kupyolera mwa Iye.

¹²⁸ Tsopano, pamene Kuwala kwakukulu uku kutulukira, kapena milozo yaikulu ya kuwala kwa Mzimu: chikondi, mtendere, ndi zonse zomwe zinalipo, Izo. Uko kunalibe kuzunkika. Uko kunalibe k—kudana, ngakhale kopanda nkhwizi; izo sizikanakhoza kubwera kuchokera mu Kasupe uyu. Uyo anali Yehova. Uyo anali Yehova Mulungu. Ndipo tsopano, monga afioroje amadzitcha izo, fiofane inapita kuchokera kwa Icho, chomwe chinkatchedwa, mwa Malemba, “Logos,” Logos yomwe inapita kuchokera kwa Mulungu. Ndi kovuta kuti tifotokoze, koma Iyo inali gawo la Mulungu.

¹²⁹ Tsopano, apa pali zomwe zinachitika. O, ndikhululukireni ine. I—i—ine ndikungofika pa izi, izi zikungondifikitsa ine pamene ine ndikuzikonda izo. Mukuona? Logos, ndipo Kasupe wamkulu uyu, Kasupe wamkulu uyu wa Mzimu yemwe analibe chiyambi kapena analibe mapeto; Mzimu waukulu uwu unayamba kupangika, mu chirengedwe, ndipo Logos yomwe

inatuluka kuchokera kwa Icho anali Mwana wa Mulungu. Anali mawonekedwe okha owoneka amene Mzimu unali nawo. Ndipo iyo inali fiofane, chomwe chikutanthauza thupi, ndipo thupilo linali ngati munthu.

¹³⁰ Mose analiwona Ilo pamene Ilo linkadutsa . . . p—pafupi ndi thanthwe. Ndipo iye anayang’ana pa Ilo, anati, “Ilo linkawoneka ngati ku nsana kwa munthu.”

Ndi thupi la mtundu womwewo limene ife timalandira pamene ife tifa kuno. “Ngati msasa wa pansu uwu usungunuka, ife tiri nawo kale wina ukudikirira.” Ilo linali Limenelo. Ndipo ilo linali fiofane yemwe anali Mwana wa Mulungu. Mwana uja, Logos ija, inadzakhalala thupi, chifukwa ife tinaikidwa mu mnofu. Ndipo fiofane, Logos, inadzakhalala mnofu, kuno pakati pathu, ndipo Iyo siinali kanthu kalikonse koma malo okhalamo, a Kasupe yense uja ankakhala mwa Iye. O, kodi inu mukuziona izo? Ndi Izo apo. Uyo anali Mmodzi, yemwe, mu . . .

¹³¹ Penyani apa. Tiyeni titembuzire tsopano mofulumira ndithu ku Ahebri, mutu wa 7, basi kwa mphindi y—ya chisomo, Mulungu pokhala akulolera. Tiyeni tiwone momwe izo zikuwonekera apa. Abrahamu!

Kodi tiri ndi nthawi yochuluka bwanji? Ife tiri ndi maminiti khumi. Chabwino. Ife titenga izi, ndiye ife titsiriza izo, wotsatira, kapena Lamlungu, Ambuye akalola.

¹³² Abrahamu anali akubwerera kuchokera kokapha mfumu.

Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, . . .

Ndi angati akudziwa komwe, yemwe, chomwe Salemu anali? Yerusalemu.

. . .mfumu ya Salemu, kalonga wa Mulungu wammwambawamba, yemwe anakomana ndi Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mafumu, ndipo anamudalitsa iye;

Mvetserani.

Kwa yemwenso Abrahamu anapereka gawo lakhumi la zonse; poyamba pakuti mwa kutanthauzira ndi Mfumu ya chilungamo, . . . pambuyo pa izonso Mfumu ya Salemu, yomwe ili, Mfumu ya mtendere;

Wopanda bambo, wopanda mayi, wopanda mtundu wochokerako, wopanda ngakhale chiyambi cha masiku, ngakhale kutha kwa moyo; . . .

¹³³ Mfumu inabwera uko kuchokera ku Salemu, ndipo anakomana ndi Abrahamu akubwera kuchokera kokapha mafumu. Ndipo Mfumu iyi inali yopanda bambo, inali yopanda mayi, inali yopanda chiyambi cha masiku kapena kutha kwa Moyu. Kodi Abrahamu anakomana ndi ndani? Tsopano taganizani. Iye anali wopanda bambo; Iye anali wopanda

amake. Iye analibe nthawi yomwe iye anayambira, ndipo Iye alibe nthawi yomwe Iye ati adzathere, kotero Mfumu yomweyo ya Salemu iyenera kuti ikhale ili ya moyo lero. Amen. Inu mukuziwona izi? Inali fiofane ija yomwe inali Mwana wa Mulungu uja. Salemu uti? Yerusalemu uja yemwe ali Mmwambamo, yemwe Abrahamu, pokhala atadalitsidwa, anali akumufunafuna, kuti ampeze, akuyesera kuti awupeze Mzinda womwe Wowumanga wake ndi Wowupanga anali Mulungu. Iye anayendayenda mu zikopa za nkhosa ndi mu zikopa za mbuzi, kulikonse, wopanda pokhala, akuyendayenda, ndipo anali akufunafuna Mzinda womwe Wowumanga ndi Wowupanga wake anali Mulungu. Ndipo iye anakomana ndi Mfumu ya Salemu uyo, atabwera pansi, ndipo iye anamulipira Iye gawo la khumi la zake zonse. Amen. Ndi Ameneyo. O, M'bale Graham, ameneyo anali Iyeyo. Ameneyo anali Iyeyo.

Abrahamu anamuwona Iye kachiwiri. Tsiku lina iye anali atakhala mu hema. Iye anayang'ana, akubwera cha uko, ndipo iye anawawona amuna atatu akubwera.

¹³⁴ Inu mukudziwa, basi pali chinachake chokhudza Mkhristu, kuti iye amawudziwa Mzimu pamene iye awuwona Iwo. Pamene iye. . . Iye anangowudziwa iwo. Pali chinachake basi Chazimu cha izo. Zinthu Zauzimu zimazindikiridwa Mwauzimu. Inu mukudziwa. Eya, iye akhoza kungoudziwa iwo, ngati iye anabadwa kwenikweni. “Nkhosa zanga zimalidziwa Liwu Langa.”

¹³⁵ Ndipo iye anangodziwa kuti pali chinachake. Iye anathamangira panja. Iye anati, “Bwerani muno, Mbuye wanga. Khalani pansi. Imani pang'ono pokha. Ine ndikutengerani nthongo ya mkate ndi kuyiika mdzanja Lanu. Ine ndikutsukani mapazi Anu. Dzipumitseni nokha, kenako muzipitirira ndi ulendo Wanuwu, chifukwa I—Inu mwabwera kudzandichezera ine.” Uko mu dziko lowumalo, kutenga njira yovuta, njira ya onyozeka apang'ono a Ambuye.

Pamene, Loti anali kukhala moyo mwa zolemereza, mdzukulwa wake kumusi uko, koma iye anali akukhala mu tchimo. Ndi chimene kulemera kochulukuka kumabala ndi tchimo.

¹³⁶ Kotero Abrahamu anawabweretsera iwo uko, pamene iye anakapeza madzi pang'ono ndipo anawatsuka mapazi Awo. Iye anathamangira ku ng'ombe, ndipo anakapeza ng'ombe yonenepa mu gululo, ndipo anaipha iyo; naipereka iyo kwa wantchito, kuti akaisende iyo. Ndipo anati, “Sarah, pota ufa wako.”

Inu mukudziwa chomwe kupota, komwe kuli, kumatanthauza. Inu mukudziwa, amayi anali ndi chokhala ngati mphero, chakale, iwo anali nacho mu—msuko wa ufa. Kodi inu munayamba mwawonapo chimodzi cha izo chokhala ndi mphero? Ndipo iwe umakhala ndi mpheroy mmenemo, iwe umapera ufawo, inu mukudziwa; ndipo chimakhala cholemerera

monga *choncho*, ndi kumaupera iwo, monga *choncho*. Ine ndawawonapo amayi akuchita zimenezo, nthawi zambiri, mphero, amakhala ndi kanthu kakang'ono kozungulira komwe kamakhala ndi waya wosefera pa icho. Iwo amakhoza kutenga ufawo ndi kuwusefa iwo monga *choncho*, inu mukudziwa, ndi kuwusisitira iwo mmbuyo ndi mtsogolo, monga *choncho*. Ndiye nkutenga mpheroyoyi ndi kuwupera iwo mozungulira, monga *choncho*, kuti wonse upangike. Ndipo apo ndi pamene ife timayenera kuti tipite ndi kukaperesa ufa wathu ku chigayo chakale; ndi zoperedwa zamisere zakale, inu mukudziwa, zamphamvu, ufa weniweni wa chimanga. Inu mukhoza kucheka zipika utali wa tsiku lonse, pa iwo.

¹³⁷ Kotero ndiye, anati, “Pota ufa wina, mofulumira. Ndi kupanga zikondamoyo zina komwe kuno pa moto, mofulumira ndithu.” Ndipo iwo anaikama ng'ombe ndipo anatengapo mkaka. Ndipo iwo anawutenga, anawukonza iwo, ndipo anapezapo batala. Ndiyeno iwo anapita nakaphapo ng'ombe napezapo nyama, ndipo iwo anaikazinga nyamayo. Anatenga batala wa mkaka, chigumu cha chimanga, ndipo anatenga batala kuti amuike pa zigumu zamotozo. O, izo ndi zabwino kwenikweni. Ndipo iwo anamupaka iye yense pamenepo. Ndipo iye anazitulutsa izo, ndipo anakaziika izo apo kwa Amuna atatu awa.

¹³⁸ Ndipo pamene Iwo anali kudya, Iwo ankapitiriza kuyang'ana chaku Sodomu. Ndipo patapita kanthawi, Iwo ananyamuka ndipo anayamba kuyenda nachokapo. Ndipo anati, Abrahamu, anati, “Inu simubisa izo kwa ine.”

¹³⁹ “Ine sindingakhoze kukubisila iwe chomwe Ine ndikuti ndikachite. Ine ndikupita kumusi uko. Machimo a Sodomu afika mu khutu Langa.”

Kodi Mwamuna ameneyo anali ndani? Fumbi palipose pa zovala Zake, ndipo atakhala apo akudya mnofu wa ng'ombe yaing'ono, ndi kumamwa mkaka wa ng'ombe, ndi kumadya zigumu zina za chimanga, ndi batala wina. Kodi Munthu wachirendo uyu ndi ndani? Awiri, kapena atatu a Iwo, atakhala apo. Fumbi liri palipose pa zovala Zake. O, eya, “Ndife ochokera ku Dziko lakutali.” Eya, kutali komwe. Ndipo kotero Iye anati . . . Chabwino, kodi Anali ndani Iwowo?

¹⁴⁰ Iye anati, “Ine sindingakhoze kumubisira izo Abrahamu, powona kuti iye ndi wolandira dziko lapansi.” Amen. “Ine ndimaulula zinsinsi Zanga,” mwa mawu ena, “kwa iwo omwe ali olandira nawo dziko lapansi.” Apo ndi pamene Mpingo ukuyenera kukhala uli lero. Ndiko kulondola. Kupeza Zinsinsi za Mulungu, kudziwa momwe ungasizigwirire wekha, ndi kumachitapo, ndi choti uzichita, ndi momwe ungamayendere, ndi momwe ungamakhalire moyo. Ndife olandira dziko lapansi. Kulondola. Iye akuwulula Izo kwa inu, chifukwa Iye

sangabise chirichonse. Ndicho chifukwa ife tikupenya zinthu izi zikuchitika.

Dziko likumati, “Aha, ilo ndi gulu la otentheka.” Asiyeni iwo azinena izo. Olandira dziko lapansi akuzidziwa zinthu izi. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

. . . pakuti iwo azidzatchedwa ana a Mulungu.

Odala ali iwo omwe ali ofatsa: pakuti iwo adzalandira dziko lapansi.

Iye amadziwitsa zinsinsi Zake kwa iwo, amawululira izo kwa iwo, kuwasonyeza iwo zoti azichita ndi momwe angamakhalire moyo, kusiya zinthu za mdziko; kumayenda mwaumulungu ndi kumakhala moyo mwaumulungu, mu dziko ili lapanoli, akuyenda limodzi ndi Iye. Siyani dziko lizinena zomwe iwo akuzifuna.

141 Kotero Iye anati, “Ine sindingakhoze kubisa chinsinsi ichi kwa Abrahamu, chifukwa, powona kuti iye ndi wolandira dziko lapansi. Koma,” Iye anati, “ine ndikupita kumeneko kuti ndikamuwononge Sodomu. Ine ndikupita kumeneko.”

142 “Kodi inu mukachita chiani, Bambo? Kodi Inu mwachokera kuti? Kodi zonsezi nza chiani?”

143 Anabwera pozindikira kuti, Iye anati, “Ndipo chinthu china, Abrahamu, iwe wadikirira zaka twente-faifi kwa lonjezo ili lomwe ine ndakupatsa iwe. Iwe unapeza kale matewela, m—maphinifolo ndi chirichonse, cha mwana uyu, zaka twente faifi zapitazo. Iwe wakhala ukuyembekezerabe pa Ine. Tsopano ine ndidzakuhezera iwe, basi pafupi nthawi ya moyo, molingana, ndi nthawi ya moyo, mwezi wa mawa ine ndidzakhala ndi iwe.”

144 Ndipo Sara, kuseri mu hema. Ndipo Munthu uyu anali atalozesa nsana Wake ku hema, akuyankhula kwa Abrahamu, monga *chonchi*. Ndipo Sarah anati, “Nhu!”

145 Iye anati, “Nchiyani chamupangitsa Sara kuti aseke?” Ho-ho-ho! Nanga bwanji zimenezo? Uko ndithudi kunali kuwerenga maganizo, sichoncho uko? “Nchiani chamupangitsa Sara kuti aseke?”

Sara anati, “Ayi. Ine sindinaseke konse.”

146 Anati, “O, inde, iwe unatero.” Iye anali atawopsyzedwa. Iye anali akunjenjemera. Anali Ndani Ameneyo, wodziwa zomwe iye anali kuchita kuseri mu hema? Ameneyo ndi Mulungu Yemweyu yemwe ali ndi ife lero. Mmodzi yemweyo. Iye amadziwa zonse za izo. Mukuona? Iye amangowulula izo pamene inu mukuzisowa. Mukuona?

147 “Ukuseka chiani iwe?” Mwaona, nsana Wake atatembenezikira kwa iyo. Baibulo linafotokoza zimenezo, kuti, “Nsana wake unali utatembenezidwira ku hema.” Koma, Iye

ankadziwa izo. “Kodi akuchita iye, kumbuyo uko, kuchita *izi*, inu mukuona?”

Kotero, Iye anati, “Ine ndidzakuchezerani inu.”

148 Kodi Munthu wodabwitsa uyu ndi ndani? Inu mukudziwa zomwe zinachitika? Iye anayenda mpaka uko komwe ndipo anasowa. Ndipo Baibulo linanena kuti Uyo anali Mulungu Wamphamvuzonse, Yehova, Kasupe wamkulu uja, Fiofane ija, Logosi ija.

149 Mlaliki wina ananena kwa ine, nthawi ina kale, anati, “M’bale Branham, inu simukanaganiza kwenikweni kuti uyo anali Mulungu, mungatero inu?”

150 Ine ndinati, “Baibulo linati Uyo anali Mulungu, Elohim.” Chomwe, Iye anali Mulungu Wamphamvuzonse, El Shaddai, uko nkulondola, Wopereka-Nyonga, Wokhutitsa. Amen.

151 O, ine ndikumverera mwachipembedzo! Taganizani za izo, apa, pomwe Iye ali tsopano. Ine ndikusonyezani inu Yemwe Iye ali, ndiye inu muwona Yemwe Mwanayo ali. Uyo anali Yesu, Iye asanakhale ndi Dzina laumunthu, “Yesu.”

152 Anaima apo pa kasupe tsiku lija. Ndipo iwo anali onse akumwa, inu mukudziwa, ndipo, “Kumakhala ndi madzi omwe anali mu chipululu,” ndi zinthu monga izo. Iye anati, “Two anali kudya mana.” Ananena, iye anati, “Makolo athu ankadya mana mu chipululu, kwa zaka forte.”

153 Iye anati, “Ndipo iwo, mmodzi aliyense, anafa.” Anati, “Ine ndine Mkate wa Moyo umene wabwera kuchokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba. Iye amene adya Mkate uwu sadzafa konse.”

154 Anati, “Chabwino, makolo athu anamwa kuchokera kwa Mzimu, kuchokera ku Thanthwe lauzimu lomwe linali mu chipululu, lomwe linkawatsatira iwo.”

155 Iye anati, “Ine ndine Thanthwe limenelo.” Ulemerero! Yohane Woyera, mutu wa 6.

“Bwanji,” iwo anati, “chiani?”

“Inde. Ndiko kulondola.”

156 “Bwanji,” iye anati, “Inu . . . Iwe sunafike ngakhale usinkhu wa zaka fifite.” Ndithudi, ntchito Yake inkamupanga Iye kuwoneka wokalambirapo pang’ono, koma Iye anali sate zokha. Anati, “Ndiwe mwamuna wosakwana nkomwe usinkhu wa zaka fifite zakubadwa, ndipo Iwe ukuti Iwe unamuwona Abrahamu, yemwe wakhala atafa kwa zaka mazana eyiti kapena naini? Ife tikudziwa tsopano kuti Ndiwe mdierekezi.”

157 Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.” Ndi Uyo apo. Kodi INE NDINE anali ndani? Dzina lopitirira kwa mibadwo yonse. Ilo linali . . . Lawi la Moto lija mu chisamba choyaka, “INE NDINE YEMWE NDIRI.” Apo Iye anali, Fiofane

ija anakomana nayo apa, yotchedwa Mwana wa Mulungu, INE NDINE, Yehova.

158 Tomasi anati, “Ambuye, tiwonetsereni ife Atate. Icho chitikhutitsa ife.”

159 Anati, “Ine ndakhala ndi inu motalika chotere, inu simukundidziwa Ine?” Anati, “Pamene inu mukundiwona Ine, inu mukuwawona Atate. Bwanji ukuti, ‘Tiwonetsereni ife, Inu, Atate?’ Ine ndi Atate tiri Mmodzi. Atate Anga akukhala mkati mwa Ine. Ine ndangokhala kachisi wotchedwa Mwana. Atate akukhala mkati mwa Ine. Si Ine yemwe ndikuchita ntchitozo, ndi Atate Anga omwe akukhala mkati mwa Ine. Iye akuchita ntchitozo, osati Ine.”

160 Tsopano, ataima kumbuyo uko, apanso, Mose anamuwona Iye, gawo la kunsana kwa Iye, anati, “Unkawoneka ngati nsana wa munthu,” Logos yomwe inachokera kwa Mulungu.

161 Ndiye nchiani chinachitika? Uyu anali Mulungu. Ndipo chifukwa chomwe Iye anachokera kwa Logos kudzakhala thupi. . . Chiani? Mmotani inu. . . Nchiani chinachitika kwa izo? Maminiti asanu izo zisanachitike, Iye anali. . . Iye anali Logos. Koma kodi Iye anachita chiani? Iye anangofikira apo. . .

162 Tsopano, matupi athu amapangidwa kuchokera ku zipangizo sikisitini zosiyana za mdziko. Ife tikudziwa zimenezo. Iwo ndi opangidwa kuchokera ku potashi, n—ndi n—ndi kashiamu pang’ono, n—ndi petroleamu, ndi kuwala kwadziko, ndi maatomu, ndi zina zotero. Zonse zikamangidwa palimodzi, ndipo zimapanga thupi ili, zimabwera kuchokera ku fumbi la dziko. Inu mumadya chakudya. Pamene inu mudyu chakudyacho, icho chimasanduka kukhala. . . kuchokera ku fumbi, ndipo icho chimachokera mu fumbi, ndi basi—icho chimangopitirira patsogolobe. Thupi lanu, kunena za thupi lanu, ilo si losiyana kwa la kavalo, kapena kwa la ng’ombe, kapena china chirichonse. Ilo ndi mnofu basi.

163 Ndipo, mnyamata, iwe umalipatsa ulemerero thupi; koma mzimu uwo uli ndi solo mkati mmenemo, m’bale wanga. Uko nkulondola. Koma thupi lako langokhala fumbi la dziko lapansi, monga chinyama. Thupi lako si lopera la chinyama. Ndipo ngati inu mumasilira thupi ndi chinthu chomwe inu mumachiwona, kusilira akazi, kusilira zinthu zina zonse izi, icho ndi chinyama apobe. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Inu musamachite izo. Mzimu wa Mulungu umakutsogolerani inu mopitirira ndi kukuikani inu pa malo apamwamba kuposa amenewo. Ndizo ndendende kulondola.

164 Tsopano, ndipo apa, Fiofane yaikulu iyi itaima apo. Chiani? Yehova Mulungu wamkulu uyo, inu mukudziwa zomwe Iye ananena? Iye anangofikira apo ndipo anatenga maatomu apang’ono okwanira mdzanja, anatenga kuwala pang’ono, ndipo

anakutsanulira iko mwa iye monga *chonchi*, anati, “Psyfuu,” thupi, ndipo anangolowa mu ilo lomwe. Ndizo zonse.

165 Anati, “Bwera kuno, Gabrielo,” Mngelowamkulu uja. Anati, “Psyfuu.” “Lowa *mnenemo*.”

166 “Bwera kuno, Mikaeli,” Mngelo waku dzanja Lake lamanja. “Psyfuu.” Pakuti . . . “Iwe lowa *mnenemo*.”

167 Mulungu, ndi Angelo awiri, anayenda pansi kuno mu thupi laumunthu, ndi kumwa mkaka wochokera kwa ng’ombe, kudya batala wochokera mu mkaka, ndi kudya zigumu zina, ndi kudya nyama ya ng’ombe yaing’ono. Angelo awiri ndi Mulungu. Baibulo linanena chomwecho. Ameneyo ndi Melkizedeki, yemwe Abrahamu anakomana naye, akubwera kuchokera kokapha mafumu. Ameneyo ndi Mwana wa Mulungu.

168 Pitirirani, kuno mu Ahebri, wa 7, anati, “Koma anapangidwa mwa dongosolo longa la Mwana wa Mulungu.” Apo Iye ali. Iye anapanga zinthu zonse ndi Iye. Ndipo Iye anayenda kumka uko komwe, ndipo anangosintha kuchoka mu kufumbi ilo nilibwera ku fumbi lomwenso, ndipo analowanso mu Ulemerero momwe.

169 Ndipo Angelo, mwamsanga pamene Iwo anamuwombola Loti ndi Akazi a Loti, ndipo iye anapitiriza kuyang’ana mmbuyo. Iye anati, anawauza iwo kuti asachite izo kachiwiri. Ndipo Iwo anapita kubwereranso—mu Kukhalapo kwa Mulungu.

170 Tsopano, ndi chiyembekezo chachikulu bwanji chomwe ife tiri nacho, Chikhulupiriro chachikulu ichi chomwe ife tikuchitumikira usikuuno! Mulungu wamoyo, Yehova, Lawi la Moto, ali ndi ife. Akudzisonyeza Yekha mu mphamvu, ndi zochita, ndi kudzikulitsa. Kuwalola iwo kuti atenge Chithunzi cha Iye, Yehova yemweyo. Mwana wa Mulungu yemwe anabwera kuchokera kwa Mulungu, anabwereranso kwa Mulungu, ndipo akukhala mu Mpingo Wake kwanthawizonse. Ndi Uyo apo.

171 Iye ali nawo maina athu pa Bukhu Lake, ali ndi lumbiriro la pa Iyeyekha, pakuti palibe wina wamkulu yemwe Iye angakhoze kulumbirirapo, kuti Iye adzatiutsa ife apo mu tsiku lotsiriza. “Iye amene adya Thupi Langa, ndi kumwa Magazi Anga, ali nawo Moyo wosatha, ndipo ine ndizamukitsa Iye pa tsiku lotsiriza. Iye amene adza kwa Ine, Ine sindidzamataya konse iye kunja. Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.”

172 Mmodzi yemwe uja angakhoze kungofikira ndi kugwira kashiamu wodzaza dzanja ndi potashi, nkuti, “Psyfuu,” ndipo ndi inu apo kachiwiri. Ndipo dzina langa liri pa Bukhu Lake. O! O! O! Ndikusamala chiani momwe mapewa anga akugwera, momwe ndikukalambira? Ndithudi ayi. Sindiri kudandaula pang’ono.

¹⁷³ M'bale Mike, limodzi la masiku awa, adalitse mtima wanu, m'bale, pamene lipenga lalikulu ilo liti lidzabwere, kumveka uko, ndipo Yosefe uyo adzabwera apo. Aleluya! Iye adzati, "Ana!" "Psyfuu." Apo inu mudzakhala muli, mutapangidwa mu mawonekedwe Ake; aang'ono kwanthawizonse, usinkhu wa ukalamba wapita kutali; matenda, mavuto, zisoni zasowa. Ulemerero ukhale kwa Mulungu wamoyo!

¹⁷⁴ Uyo ndi Yemwe Iye akuyankhuliramo, lero, Mwana Wake. "Mu nthawi Zakale ndi mmachitidwe osiyana Iye ankeyankhula kupyolera mwa mneneri, koma mu tsiku lotsiriza lino kupyolera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu." Iye akuyankhula kwa mtima wa munthu aliyense yemwe Iye wamuitana. Ngati inu munayamba mwamvererapo konse Liwu Lake kapena munamvapo kugogoda Kwake pa mtima wanu, chonde musakukane Iko kuchoke.

Tiyeni ife tipemphere.

¹⁷⁵ Atate Akumwamba, usikuuno, pamene ife tiri okondwa kwambiri kudziwa, pa kutsegula kwa Kalata ya Ahebri iyi, momwe Paulo anapitira mmbuyo momwe ku Mauthenga. Iye sakanati angozitengera izo pa zongomva kapena pa chomuchitikira. Iye ankafuna kuti ife tizidzadziwa chomwe chinali Choonadi. Ndipo iye anapita mmbuyo momwe mu Mauthenga, ndipo iye. . . kubwerera mu Chipangano Chakale, Uthenga womwe unalalikidwa kwa iwo. Ndipo iye anawona, kudzera mu Chipangano Chakale apo, mithunzi yonse ndi zoimira. Ndi chifukwa ife tiri ndi Bukhu lalikulu ili la Ahebri usikuuno. Ndipo ife tikuliwona Ilo, Ambuye, ndipo ife tikulikonda Ilo. Ndipo kupyola mu mibadwo, Ilo lawotchedwa, Ilo lamwazidwa, Ilo layesedwa kuti lithetsedwepo, koma Iye akudutsa mafunde chimodzimidzi basi. Pakuti Inu munati, "Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzatero."

¹⁷⁶ Ndiye wokaikira angati, "Chabwino, inu munati, 'Paulo analemba izi.'" Osati Paulo, koma Mulungu yemwe anali mwa Paulo; Chokhalapo cholenga chija chomwe chinali mkati mwa Paulo.

¹⁷⁷ Basi monga chinali mwa Davide, pamene iye anati, "Ine sindidzalola Woyera Wanga kuti awone chivundi, ngakhalenso sindidzawusiya moyo Wake mu hade." Ndipo Mwana wa Mulungu anawatenga Mawu awo kuchokera kwa mneneri ameneyo, ndipo anapita pansu mu chifuwa cha gehena chomwe. Ndipo anati, "Phwasulani kachisi uyu, ndipo Ine ndidzamuukitsa Iye mu masiku atatu." Ndipo Iye anazichita izo, chifukwa Mawu a Mulungu sangakhoze kulephera. Dontho limodzi silingakhoze kulephera. Momwe ife tikumuthokozera Mulungu pa izi, Urimu Tumimu wamkulu uyu, ndipo kudziwa kuti zotichitikira zathu usikuuno, Ambuye, zikuwalira pa

Baibulo ili lomwe apa! Ndife obadwa kachiwiri, tiri nawo Mzimu Woyera.

178 Wokonedwa Mulungu, ngati pangakhale pali mwamuna kapena mkazi muno usikuuno, mnyamata kapena msungwana, yemwe sanayambe wachitirapo umboni izi, iwo angakhoze bwanji kuwuka ngati mulibemo Moyo mmenemo? O, iwo akuti, “Ine ndiri nawo Moyo.”

179 Koma Baibulo linati, “Iye yemwe akhala mu chisangalatso ndi wakufa pamene iye akanali moyo.” Inu mukuti inu muli nawo Moyo, koma ndinu okufa. “Inu mumadzinenera,” linatero Baibulo, “kuti inu muli nawo Moyo, koma ndinu okufa. Ngakhale inu mukuti ndinu olemera ndipo simukusowa kanthu; koma simukudziwa kuti ndinu omvetsa chisoni, ndi osauka, ndi amaliseche, ndi akhungu, ndipo simukudziwa izo.” Ndipo icho ndi chikhaliidwe cha mipingo usikuuno, Ambuye. Momwe iwo akuphonyera zinthu zazikulu, zaphindu izi.

Kudziwa kuti Mulungu Yehova wamkulu, Yemwe angakhoze kokha kupereka mwa...Iye anati, “Ndibweretsereni inu tinsomba tating’ono ito.” Iye ankayenera kuti atenge nsomba k—kuti apange chinachake ndi izo. Kusonyeza, kuti chiukitsiro chinkayenera kuti chikhale chinachake, choti achite nacho chinachake. Iye sanangopanga nsomba zokha, koma iye anapanga nsomba zophikidwa; Iye, mkate wophika. Ndipo Iye anadyetsa zikwi zisanu ndi nsomba zisanu zazing’ono, mikate yaing’ono ndi nsomba ziwiri. O Ambuye, izo zinali mu manja Ake, ndipo Iye anali Mlengi. Koma Iye ankayenera kuti akhale ndi chinachake mdzanja Lake.

Mulungu, mulole ife tidzigoneke tokha mu manja Ake, usikuuno, nkuti, “O Mulungu, nditengeni ine momwe ine ndiriri. Ndipo pamene mathero a moyo wanga adzakhala pano, mundirole ine ndipite ndi chiyembekezo ichi chomwe chinali mkati mwanga, podziwa kuti ine ndabadwa kachiwiri, ndipo Mzimu Wanu wachitira umboni ndi ine, ndipo wachitira umboni ndi mzimu wanga, kuti ndine Mwana Wanu, kapena Mwana Wanu wamkazi.” Ndipo pa tsiku lotsiriza ilo, Inu mudzawaukitsa iwo. Perekani izi, Atate.

180 Ndipo pomwe ife tiri ndi mitu yathu itaweramitsidwa, ngati pangakhale mmodzi yemwe angakweze dzanja lake, ndi kuti, “Ndikumbukireni ine, M’bale Branham, mu pemphero. Ine ndikufuna Mulungu kuti andidziwe ine pamene ine... ndisanachoke panso pano, kuti Iye azindidziwa ine mochuluka kwambiri kuti Iye adzaitana dzina langa. Ine ndidzayankha.” Ambuye akudalitse iwe mwananga. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu; ndi inu, dona. Winawakenso? Ingokwezani dzanja lanu. Nkuti, “Ndipemphererani ine, M’bale Branham.” Ndi chimene ife titi tichite. Mulungu akudalitse iwe, dona wamng’ono. Ndizo zabwino.

¹⁸¹ Tsopano, pomwe mutu wanu waweramitsidwa, mukupemphera, ine ndikuti ndiyimbe ndime ya nyimbo iyi.

Usakhumbe chuma cha mdziko,
Chomwe chivunda mwamsanga,
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Izo sizidzathapo.
Gwira dzanja la Mulungu.
Gwira dzanja la Mulungu.
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Gwira dzanja la Mulungu.

¹⁸² Pamene iye akuisewera tsopano, ndi mutu wanu woweramitsidwa, kodi inu mungangofikira ndi dzanja lanu mmwamba, nkuti, “Inde, Ambuye, langa ndi ili”? Kodi izo zikanachita chiani? Ilo lisonyeza mzimu wanu, mkati mwanu, wapanga lingaliro. “Ine ndikufuna dzanja lanu, Ambuye.” Mulungu akudalitse iwe, msungwana wamng’ono. “Ine ndikukweza dzanja langa.” Mulungu akudalitse iwe, msungwana wamng’ono, pansi apa. Izo nzabwino, wokonedwa. Mulungu, iwe ukudziwa, ndi wokondwa kukuwona iwe ukuchita izo. “Lolani ana aang’ono adze kwa ine.”

¹⁸³ “Ine ndikufuna, Mulungu, Inu mugwire dzanja langa. Ndipo pa tsiku limenelo, ine ndikufuna kuti ndidzakhale mu dzanja Lanu; kuti, pamene Inu mudzaitana, ine ndidzabwere.” Inde, monga Lazaro anachitira. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

Ulendo wanu ukadzatha,
Kwa Mulungu tikakhala woona,
Kwanu kowala mu Ulemerero,
Moyo wanu udzakwatulidwa.

Kodi inu muchite chiani tsopano, ndiye?

Gwira dzanja la Mulungu.
Gwira dzanja la Mulungu.
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Gwira dzanja la Mulungu.

¹⁸⁴ Atate Akumwamba, manja angapo anakwera mmwamba, mu msonkhano waung’ono uno, usikuuno, kuti iwo akufuna agwire, usikuuno, ku dzanja Lanu losasintha, Lamuyaya. Podziwa kuti chomwe chaperekedwa kwa Inu. . . Inu munati, “Ine. . . Onse omwe Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo palibe mmodzi wa iwo ati adzataike. Ndipo ine ndidzawaukitsa iwo pa tsiku lotsiriza. Sangakhoze konse kuwonongeka, sangakhoze konse kubwera ku chiweruzo, koma ali nawo Wamuyaya, Moyo Wamuyaya.” Ndipo pali Moyo Wamuyaya umodzi wokha. Umene umabwera kuchokera kwa Mulungu, yekha. Iwo ndi Mulungu. Ndipo ife timakhala gawo la Mulungu, mochuluka choncho kuti ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Pamene ife tiri ndi Mzimu wa Mulungu mkati mwathu, ife timaganiza monga Mulungu. Ife timaganiza

za chirungamo ndi chiyero, ndipo ife timayesera kukhala moyo moti tizimusangalatsa Iye.

¹⁸⁵ Perekani, Ambuye, kuti mtundu uwo wa Moyo ulowe mwa munthu aliyense yemwe anakweza dzanja lake. Ndi iwo omwe akanati akweze manja awo, ndipo sanatero, ine ndikupemphera kuti Inu mukhale nawo iwo. Perekani izi, Atate. Ndipo pamene ulendo watha, moyo watha, mulole ife tidzakalowe mu mtendere pa tsiku limenelo, limodzi ndi Iye, komwe ife sitidzakalamba konse, sitidzadzala konse, sikudzakhala konse vuto. Kufikira pamenepo, tisungeni ife achisangalalo ndi okondwa, tikumutamanda Iye, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

¹⁸⁶ Nonse inu okhulupirira, tsopano, tiyeni tingokweza manja athu mmwamba ndi kumaimba korasi ija.

Gwira dzanja la Mulungu.
Gwira dzanja la Mulungu.
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Gwira dzanja la Mulungu.

Tsopano tiyeni tiziyung'uzza iyo. [M'bale Branham akuyamba kung'ungu'za *Gwira dzanja la Mulungu*—Mkonzi.]

¹⁸⁷ Pamene inu mukuchita izo, oyandikana nawo anu; inu muziti, “Mulungu akudalitseni inu, woyandikana nane.” Gwiranani chanza ndi winawake wakhala pafupi ndi inu. “Mulungu akudalitseni inu.” Mmbali zonse ziwiri tsopano. Kumbali zonse ziwiri, gwiranani manja. “Mulungu akudalitseni inu, woyandikana nane. Mulungu akhale ndi inu.” Mangani ziyembekezo zanu pa zinthu Zamuyaya.

Doc, ine ndikudziwa ziri apo, m'bale. Ine ndikudziwa inu mwakhala muli pamenepo, M'bale Neville, nthawi yaitali.

Pamene ulendo udzatha,
Zidzachitika, limodzi la masiku amenewa.
Kwa Mulungu tikakhala owona,
Ife tidzakamuwona M'bale Seward uko.

Kwanu, kwanu mu Ulemerero,
Moyo wanu udzakwatulidwa.
Gwira dzanja la Mulungu.

Ine ndimakonda kupembeda kumeneko, ukatha uthenga.

Gwira dzanja la Mulungu.
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Gwira dzanja la Mulungu.
Nthawi yadzaza ndi zosinthika,
Palibe chosasuntha chingame,
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Gwirani . . .

Tiyeni ife tigwire mawonekedwe a Iye, Uyo wosawonekayo pakati pathu tsopano, ndipo tingomupembedza Iye tsopano pamene ife tikuimba.

Gwira dzanja la Mulungu.
Gwira dzanja la Mulungu.
Manga ziyembekezo pa Zamuyaya,
Gwira dzanja la Mulungu.
Mtendere! Mtendere! wodabwitsa,

Zingompembedzani Iye tsopano.

Kubwera pansi . . .

Uthenga watha. Ndi kupembedza.

Sesani pa mzimu wathu, ine ndipempha,
Mu kuya kwa chikondi.

Zingomasambani mwa Iye.

Mtendere! Mtendere! wodabwitsa,
Kutsika pansi kuchokera . . .

Kasupe wamkulu uja, Iye akutsegukano.

. . .mmwamba;
Sesani pa mzimu wathu, ndipempha,
Mu kuya kwa chikondi.

Kodi izo sizikuchita chinachake basi?

Mtendere wodabwitsa,
Kuchokera kwa Atate athu Mmwamba;
Sesani pa mzimu wathu, ndipempha,
Mu kuya kwa chikondi.


Kodi palibe chinachake cha Iwo, chokhathamira basi ndi chokoma?

¹⁸⁸ Ndipo ine ndikudabwa ngati pali munthu wodwala yemwe akufuna kuti adzozedwe ndi kupemphereredwa. Ngati alipo, ingopeza malo anu. Kodi ndi dona uyo mu chikuku apo? Ingosiyani iye akhale pomwepo. Ine ndibwera, kudzamupempherera iye. Iye sasowa kuti anyamuke mu chikukumo. Winanso? Chabwino.

O, kodi inu simukulikonda gawo ili la msonkhano? Ndi angati akumverera, akungodziwa kuti Kukhalapo kwa Mulungu kuli pano? Ndicho chimene ine ndimachikamba. Mofanana choncho...Inu mumangomverera ngati...Ndi angati akumverera ngati kuti inu mungofuula mokweza? Tsopano tiyeni tingowona. Ndikungomverera ngati ndi chinachake, chomwe iwe ungafune, kuti ungofuula mokweza. Mukuona?

Mtendere! Mtendere! wodabwitsa,
 Kuchokera kwa Atate Mmwamba;
 Sesani pa mzimu wanga, ndipempha,
 Mu kuya kwa chikondi.
 Muwale pa ine,

¹⁸⁹ Pamene ife tiri mu kupembedza, ife tikuti tiwadzoze odwala tsopano, ndi kuwapempherera iwo. Kodi inu simungabwere njira iyi, dona?

¹⁹⁰ Kodi ichi chikutanthauza chiani? “Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala.” Aliyense mu pemphero tsopano, muzingoying’ung’uza nyimbo imeneyo. Muzingoganiza za Yesu akuchiritsa odwala. Kumudzoza iye ndi mafuta. 

BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org